# *Israeli Ndi Mpingo* [1]

. . .kachisi wamng'ono wakale. Ndipo ine ndabwererako nthawi zambiri, ora kapena awiri, kapena mwinamwake kudzakhala mu msonkhano. Iyi ndi nthawi yanga yoyamba kuti ndibwerere, kapena kulikonseko, kudzayesera kuchita chitsitsimutso. Ife tikuyamba usikuuno. Chitsitsimutso, mwa kulingalira kwanga, sichimakhala, chabwino, kubweretsa mamembala atsopano. Chitsitsimutso sichimakhala gulu la otembenuka mtima, ngakhale zinthu zimenezo zimayendera limodzi ndi chitsitsimutso. Koma *chitsitsimutso* ndi "kutsitsimutsa chimene uli nacho kale," kungowatsitsimutsa iwo.

2 Ndipo tsopano ife tiri ndi m'busa wodabwitsa kwambiri pano, M'bale Neville, yemwe wakhala pa mpando kutsogolo kumene, wosasa mawu pang'ono usikuuno, chifukwa cha kuzizira.

3 Ndipo ine ndiziyika izi kwathu kwenikweni. Ine ndinali, pamene ine ndinali kuno, ine ndinali m'busa, ine ndinali wotsogolera nyimbo, Ine ndinkatenga zopereka, ine ndinkalipira ngongole, ine ndinali wosamalira pamalo pano, ndipo ine ndinali kalipentala, ndipo ine ndinkangotsuka phulusa mu chitofu, ndi kuchita chirichonse chimene chinkabwera kuti chichitidwe. Ndikatero ndimakagwira ntchito ku Public Service Company kumbali. Zaka seventini za izo, ine ndinali kuno. Ndipo ndine wokondwa kwambiri chifukwa cha kanyumba kakang'ono kachikale aka usikuuno. Ndipo ndithudi ali ngati malo obadwira kwa ine. Osati olongosoka kwenikweni, koma si aakulu; koma ndi kwathu, ndipo ine ndimamva bwino kwambiri. Ndipo ndine wokondwa kwambiri chifukwa cha izo.

4 Ndipo, tsopano, misonkhano yathu ikhala mwinamwake (ife tapereka) kwa mausiku faivi, mpaka Lamlungu usiku. Ndipo ife tiziphunzitsa kuchokera mu Malemba, kuphunzitsa. Tsopano, mu kuphunzitsa uku, iko sikukhala kwa china koma Baibulo. Tsopano, ndiyeno, ndipo mu—mu msonkhano tsopano, ine ndikufuna kuti ndizipange momveka bwino kwambiri, kuyambira pano, kuti tikhale ndi maziko enieni. Ine ndikukhulupirira inu . . . Ife tikufuna izo poyamba, ndipo tiwona malamulo ndi malangizo, ndi zonse zomwe ife timachita, kotero kuti ife tisanakhale ndi pemphero ndikuyamba misonkhano.

5 Ndipo tsopano ine ndikulinga, ngati Ambuye alola, kuti ndiyankhule usikuuno pa *Mpingo*, mausiku faivi pa: *Mpingo*. Usiku woyamba, usikuuno, ndi *Israeli Mu Igupto*. Ndipo mawa usiku, Ambuye akalola, ndi *Uko Pa Nyanja Yofiira*. Ndiyeno usiku wotsatira, *Pamaso Pa Njoka Yamkuwa*. Kenako Loweruka

usiku, *Pa Kadesi-barnea*. Ndipo Lamlungu usiku, ife tikufuna tidzawatengere iwo, *Mu Dziko Lakwawo*. Ndipo ndizo zonse ziphunzitso za Mwamalemba. Ndipo muzibweretsa Baibulo lanu, chifukwa ife tizingokhala Lemba pa Lemba.

6 Mafoni ambiri akhala akubweramo, kuti ndipempherere odwala, ndi zina zotero. Koma ine ndakhala ngati ndazitalikira izo. Ine ndikuyesetsa kuti ndisunge malingaliro anga mosamalitsa pa zophunzitsa za Baibulo. Ndipo tsopano ine sindikudziwa chimene Ambuye wathu ati achite. Ife tikuyembekezera kuyitanidwa kutsidya kwa nyanja, kuti tipite kutsidya kwa nyanja. Ine ndimaganiza kuti imeneyi inali nthawi yopambana. Mwinamwake kuyambira pamenepo, mwinamwake M'bale Neville adzakhala ali bwino podzafika nthawi imeneyo, iye akhoza kudzatolera kuchokera apo pomwe, mwinamwake, ndi kumapitirira mu chitsitsimutso ichi. Ine ndikufuna kuchiwona icho chikupitirira kudutsa Isitara. Ndipo ine ndikufuna kudzakhala ndi ubatizo waukulu kwambiri kuno mmawa wa Isitara. Kodi zimenezo sizingakhale zodabwitsa? Nthawi basi yoti gulu lalikulu libatizidwe. Ine ndikukhulupirira kuti pali achinyamata ena pano oti abatizidwe.

7 Ndipo tsopano pamene ine ndiri pa funso la achinyamata. Tsopano, ife tiri ndi alendo pang'ono. Ine ndikuganiza kuti sindikudziwa yemwe amabwera kuno ndi yemwe samabwera. Ine basi sindikudziwa. . . [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi].

8 Mutu wa 12, kuti tiyambirepo, ndipo inu muli ndi mapensulo ndi mapepala. Ife tiri ndi Mabaibulo ena owonjezera, ngati wina angafune kutsatira Malemba ena ndipo angafune limodzi. Mmodzi wa akulu a mpingo angakhale wokondwa kulibweretsa ilo kwa inu pakali pano, ngati inu mungakweze dzanja lanu. Ife tiri nawo Mabaibulo faivi kapena sikisi pano. Enawo angokhala Chipangano Chatsopano basi, m'bale, ndipo ine ndikhala mu Chipangano Chakale kwambiri, usikuuno.

9 Mu kuwerenga kwa Lemba, ine ndimaimbidwa mlandu, ndikuchita gawo lalikulu la zofanizira. Chomwe, *typology* ndi "kufanizitsa Chakale ndi Chatsopano." Ine ndikuuzani inu chifukwa chimene ine ndimachitira izi. Ndi chifukwa cha izi.

10 Mwinamwake nthawizina ma—mawu aakulu amene masikolala ndi ena otero amayesetsa kulipatsa Baibulo Ake—mawu Ake kapena matchulidwe ake. Ndine wokhutitsidwa kutenga King James ngati langa. Ilo lagwedeza mikuntho nthawi yaitali kuposa kumasulira kulikonse, ndipo ine ndimangolikhulupirira ilo mwanjira imeneyo.

11 Ndipo ndikukhulupirira kuti Lemba lonse limaphunzitsa kuti Chipangano Chakale chonse chinali mthunzi wa zinthu ziri nkudza. Chotero, ngati ine ndikupita ku khoma limenelo, ndipo mthunzi wanga uli patsogolo panga, iwo udzalengeza

chinachake chonga chimene ine ndiri pamene ndizibwera pamenepo. Izo zingasonyeze ngati ine ndinali chirombo cha miyendo foro, kapena ngati iyo inali mbalame, kapena chirichonse chimene icho chinali, mthunzi udzafotokoza zimenezo.

12 Ndipo Chipangano Chakale chinali mthunzi kapena choyimira cha Chipangano Chatsopano. Chipangano Chakale chonse chimaloza ku Kalvare. Ine ndikukhulupirira, mothandizidwa ndi Mzimu Woyera, kuti kudutsa mu— mmasabata akubwerawa (motalika bwanji, ine sindikudziwa), koma ine ndikhoza kutsimikizira kuchokera. . .mutu uliwonse wa Chipangano Chakale unkayankhula za Yesu Khristu, ndipo chirichonse chinakwaniritsidwa mwa Iye. Ndipo ife, mwa Iye, tiri amphumphu. Ndi zophweka bwanji momwe Mulungu anazipangira izo! Mwa Khristu, ife tiri amphumphu.

13 Tsopano, munthu nthawizonse wakhala akuyesetsa kudzipulumutsa yekha, ndi kuchita zinthu zosiyanasiyana kuti apulumutsidwe nazo, koma izo sizinayambe zakhalapo, mu Chipangano Chatsopano, mwa ntchito zathu zonse, ndi "Mwa chisomo inu munapulumutsidwa, kupyolera mu chikhulupiriro." Ndicho chinthu chokhacho chimene chingakupulumutseni inu, ndicho chisomo.

14 Tsopano, ine ndinakukwezetsani manja kanthawi kapitako, posadziwa omwe ali mamembala pano a mpingo, ndi amene siali, kuti ndiwone momwe izo zikuyendera ndi Chikhristu. Ndipo zikuwoneka kuti mulipo Akhristu pafupifupi nainte-naini pa handirede pano usikuuno. Ndipo ine ndikuyembekeza kuti enawo alipo tsopano.

15 Tsopano, *Bukhu la Genesis* ndi mutu wa mbewu wa Baibulo. Chimenecho ndicho chiyambi. Mawu akuti *Genesis* amatanthauza "chiyambi."

16 Ndipo tsopano, mawa usiku, ife tiyenera kupita mu Eksodo, kuti tikawatenge ana. Ndipo mawu akuti *Eksodo* amachokera ku mawu a—a "kuitana atuluke, akutuluka." Ana anali a Israeli, anatulutsidwa. Mu eksodo wawo, iwo anatuluka mu Igupto, kupita ku dziko lolonjezedwa limene Mulungu anali atawapatsa iwo.

17 Tsopano, pofuna kuti muchipeze molondola chithunzi cha mpingo wa nthawiyo, ndi kuwufanizitsa iwo ndi lero; inu muyenera kubwerera ku mbewu, kuti mukaibweretse iyo mu eksodo, iyo isanakhale nayo eksodo. Tsopano inu. . .Kapena, kuibweretsa iyo mu. . .kumene inu mukhoza kuwona momwe mpingo uliri, ndipo momwe iwo anadzakhazikikira mu Igupto, ndiyeno inu mudzawona momwe Mulungu anawaitanira iwo atuluke. Ndiyeno kudutsa mu sabata yonseyo, ife tizipita molunjika ku Malemba monga choncho. Ndipo usikuuno ife

tikufuna kuti tigwiritse ntchito Malemba ochuluka, ochuluka, ngati Ambuye alola, pa kuphunzitsa.

18 Tsopano, malo oyambirira amene ife tikufuna kuti tiwapeze, ndi chifukwa chake. . . Ichi chakhala chinthu chachikulu kwambiri chimene ine ndachipeza pakati pa anthu Achikhristu padziko lonse lapansi, chakhala mantha. Iwo nthawizonse amachita mantha. Ndipo pamene matenda aang'ono akantha, iwo amachita mantha. Ambiri, ine ndimadabwa nthawizina, ndipo tsopano ndiri nanu limodzi. Koma tsopano chimene ine ndikuyesetsa kuti ndichite usikuuno, ndipo mu sabata imene ikubwerayi, ndi kuyesetsa kuti ndithamangitse mantha amenewo, pogwiritsa ntchito Mawu a Mulungu.

19 Tsopano, inu mukanabwera kwa ine ndi kunena kuti, "Chabwino, M'bale Branham, ine ndimakhulupirira *ichi*. Tsopano, ine ndikukhulupirira *icho*."

20 Ilipo njira imodzi yokha mu dziko yotsimikizira. Tsopano, ine sindingakhoze kuyenda pogwiritsa ntchito chomuchitikira cha winawake, mwambo wa mpingo wa winawake. Ulipo umboni umodzi wokha woona. . . wa chomwe izo zonse ziri, ndiwo Mawu a Mulungu. Tsopano, ngati Mawu a Mulungu anena chinthu chinachake, ndiye ine ndiyenera kukhulupirira kuti icho ndi Choonadi.

21 Posachedwapa panali mtumiki wachinyamata anabwera kwa ine ndipo anandiuza ine za vuto lina lake, ndipo anati iye anapempherera izo. Ndipo iye anati Ambuye anawululira kwa iye kuti inali njira inayake. Ndipo ine ndinamuyang'ana iye pang'ono, ndipo ndinati, "M'bale, izo ndi zokoma kwambiri." Ine ndinati, "Ine—ine ndikuyamikira Ambuye pokuchitirani inu zimenezo. Koma, ndiroleni ine ndikuuzeni inu chinachake, izo ndi zosiyana."

Iye anati, "Chabwino, masomphenyawo anachokera kwa Mulungu."

22 Ine ndinati, "Izo sizingakhale kuti ndi chomwecho, m'bale, chifukwa izo zinali zotsutsana ndi Mawu."

23 Tsopano, ife tiyenera kumatsimikizira zinthu zonse ndi Lemba. Osati zimene. . . Ngati Izo ziri zotsutsana ndi chikhulupiriro changa, ndipo komabe Lemba limanena chomwecho, Lemba ndi lolondola ndipo ine ndikulakwitsa. Mukuona? Lemba limakhala lolondola nthawizonse. Ndipo njira yokhayo yomwe inu mungachitire chirichonse, ndi kubwerera ku Lemba. Tsopano, kodi izo nzoona? Tsopano, ine—ine ndimakonda kukumvani inu mukuti "ameni" pamene inu mukukhulupirira Izo, inu mwaona. *Ameni* amatanthauza "zikhale chomwecho." Tsopano, ife tsopano sitingathe. . .

24 Winawake amandifunsa ine tsiku lina, chabwino, ngakhale tsiku lino, za munthu wina amene anali a—munthu wopambana

mu chinthu chinachake chimene iwo anali kuchita. Ndipo anati, "Oh, M'bale Bill, Ambuye ayenera kukhala mu zimenezo."

Ine ndinati, "Iye sangakhoze."

"Oh," anati, "iwo akupulumutsa miyoyo."

25 Ine ndinati, "Izo sizingakhoze kukhala. Chifukwa, ngati izo ziri, izo ndi zotsutsana ndi Mawu Ake. Ndiye, Mulungu sangakhoze kunena chinthu chimodzi ndipo kenako nkudzanena chinthu china. Iye azinena chinthu chimodzi kudutsa njira yonse." Mwaona, Mulungu sangakhoze kunama. Mulungu ndi wosalephera, Mawu Ake ali. Pofuna kukhala Mulungu, Iye ayenera kukhala wochita mwayekha, inu mukuona. Ndipo Iye ali.

26 Ndipo tsopano inu mukuti, "Chabwino, kodi inu simukuganiza ngati—ngati Mulungu anachita chinthu chinachake apa, ngakhale kuti Mawu Ake amati . . .?"

27 Ine ndinati, "Ayi. Baibulo linati, 'Iye amene achotsa kapena kuwonjezera pa chirichonse chimene chiri mu Bukhu ili, adzachotsedwa mu—mu Bukhu la Moyo, kwa iye.'"

28 Kotero, chifukwa chake ndi chimenecho. Nthawizonse, mwa chirichonse, osati mwa chokuchitikira, kapena osati ndi momwe icho chikuwonekera, koma ndi chimene Mawu a Mulungu ananena. Tsopano, Chipangano Chatsopano, Paulo anati, "Ngakhale ife kapena Mngelo wochokera Kumwamba atabwera ndi kudzaphunzitsa chinthu china chirichonse kuposa icho chimene inu mwachimva," ameneyo ndi Agalatiya 1:8, ngati inu mukufuna kulemba izo, "musiyeni iye akhale, kwa inu, wotembereredwa."

29 Tsopano, chotero, tiyeni tibwerere mmbuyo tsopano ndipo tikapeze chiyambi ndi kukapeza momwe Mawu awa aliri otsimikizika. Tsopano muzisunge izi mmalingaliro. Ndipo pamene ife tikukunkha mu Baibulo ili, inu muwona kuti zimano za magudumu a Mulungu zimayenda pang'onopang'ono koma motsimikizika. Zitha kuwoneka ngati ziri mtunda wa mailosi millioni, koma izo zikupera pamenepo nthawi zonse, ndipo limodzi la masiku awa zidzakhala pano, tsopano, ziribe kanthu chiyani. Inu mungotenga lirilonse la . . .

30 Ndikukhumba ife tikanakhala ndi nthawi tsopano yokhala ndi phunziro la Baibulo la miyezi sikisi kapena eyiti pano, kuti tidzatenge Bukhu la Genesis ndipo osachoka konse ku Genesis. Ndipo ine ndikukhulupirira, mkati mwa masabata atatu, atatu kapena foro otsatira a kuphunzira mu Genesis, ndi kuwona momwe ulusi uliwonse wa izo umapitira mpaka kudutsa mu Baibulo, Mawu aliwonse a izo. Tsopano, ine ndakhala ndi zaka ziwiri zomwe ine ndakhala ndikuphunzira mu Genesis tsopano, inemwini, ndipo ndikadali pa nthawi yanga yachiwiri panobe ndikudutsa mu izo ndipo sindinadutse nkomwe theka kachiwiri.

Bwanji, izo zakhala ziri, ine ndatenga masabata pa ndime ziwiri kapena zitatu zokha. Ndipo mupeza kuti mu mbewu imeneyo . . .

31 Ngati mukufuna kuti mudziwe mtundu wa mbewu yomwe inu mudzakhale nayo, kapena chimene ichi chikumera mmunda, mubwerere kuti mukapeze chomwe mbewuyo ili. Mbewu idzabala chimodzimodzi basi chomwe iyo ili. Iyo idzabereka za mtundu wake. Chimanga chidzabereka chimanga; chisoso, chisoso; tirigu, tirigu. Chirichonse chimene icho chiri, icho chidzabala chimodzimodzi chimene mbewuyo inali.

32 Ndipo miyambo yonse iyi ndi zowukirana, ndi zinthu zonse izi ndi timalingaliro lero, mwa chisomo cha Mulungu ndizo, chirichonse, chinalembedwa mu Genesis, kumene icho chinali ndi chiyambi chake kumbuyo uko, ndipo icho changokhala ndi dzina lina. Koma inu mumayang'ana kugwira ntchito kwa mzimu mu tsiku limenelo, ndipo penyani momwe iwo ukugwirira ntchito lero, ndipo inu muwona kuti ndi chinthu chomwecho. Ndipo, abwenzi, zina za izo ndi zokhudza! Inu mukhoza kudabwa kudziwa kuti zina mwa izo ziri mmatchalitchi apamwamba kwambiri.

33 Tsopano, tangoyang'anani pa mzimu umenewo, momwe iwo unawukira kumbuyo uko mwa Kaini, momwe iwo unadzera mpaka mmusi kudzera mwa Hamu, kumapitirira kudutsa mwa Nimrodi, mpaka ku Babeloni; kuchokera ku Babeloni, kubwera mpaka mmusi mmasiku a kudza kwa Yesu. Aphunzitsi, ophunzira Baibulo, ndipo iwo analephera kuwazindikira Ambuye Yesu Khristu. Ndipo apo iwo anali atayima pamenepo, masikolala opukutidwa, amuna oyera, olungama, owadziwa Mawu, basi chilembo chirichonse cha Iwo, ndi kumene Iwo anali ndi momwe Iwo analembedwera, ankawadziwa Iwo pa mtima, onse ndi onse, mpukutu uliwonse ndi chirichonse, amayenera kubadwa mumzere winawake wa anthu, kapena unsembe, kubwera, kapena—kapena fuko, kubwera mmenemo kuti adzakhale wansembe. Akatswiri opukutidwa, ophunzira akuseminare lero angakhale nambala yambuyo kwa mmodzi wa iwo, ndipo, komabe, analephera kumudziwa Yesu. Ndipo pamene Yesu anabwera, iwo anali anthu oyera, ndipo Yesu anati, "Inu ndinu ochokera kwa atate wanu, mdierekezi." Anati, "Inu mukulakwitsa, posadziwa mphamvu ya Mulungu, ngakhale Mawu a Mulungu." Kodi inu mungalingalire Ambuye Yesu Khristu akumutcha woyera, sikolala wolungama, wophunzira Baibulo, "mdierekezi"? Koma Iye anatero. Ndipo tsopano ngati inu mungabwerere mmbuyo, inu mupeza kumene izo zinachokera.

34 Ndipo, penyani, izo zikuyenda chomwecho lero mu mphamvu yowopsya. Oh, zikukuyenerani inu, m'bale wanga, mlongo, kuti muganizire zomwe inu mukuzimvetsera, ndipo musapeputse mphamvu ya Satana pakunyenga. Inu musamamupeputse konse iye. Iye ndi wosalala monga iye

angakhoze kukhalira. Ndipo mzimu wotsutsakhristu si Chikominisi. Ayi. Mzimu wotsutsakhristu ndi wofanana kwambiri monga chinthu chenichenicho mpaka iwo udzanyenga Osankhidwa omwe ngati nkotheka. Yesu ananena chomwecho, Mateyu 24. Ndi mzimu wachipembedzo. Oh, bwanji, Kaini ndi Abele anali abale. Khwangwala ndi nkhunda zinakhala pa chisa chimodzi. Esau ndi Yakobo anali abale. Yudasi ndi Yesu anali mu mpingo umodzi, Mmodzi Mlaliki ndipo mmodzi winayo msungichuma. Mwaona pamenepo, nthawizonse kumangonyenga. Bodza limene Kaini . . . limene Satana anamuuza Eva, linali Choonadi nainte peresenti, nainte peresenti Choonadi. Ndipo bodza limene inu munganene! Momwe ine ndawamvera anthu akulambalala zidutswa mu Lemba, kuti angopewa . . . Izo zimapweteka zafioloje zawo. Mukuona? Koma ngati—ngati—ngati gawo *ili* ndi lolondola, gawo *ilo* ndi lolondola! Tiyeni tiziyike izo pamodzi ndipo tizipange izo kuti zigwirizane ndi Baibulo lonse. Tsopano, pachiyambi pamene Mulungu . . .

35 Ife sitikhala ndi nthawi mu izi, kuti tibwerere kumeneko, koma ife tiyambire pamwamba apa pa chiyambi cha mpingo. Ndipo apo panali pamene Mulungu . . . Tsopano, mawu oti *mpingo* amatanthauza "oyitanidwa atuluke, anthu oyitanidwa atuluke." Ndipo ine ndikukhulupirira, mu chipembedzo chirichonse pansi pa kumwamba lero, payenera kukhala pali anthu ena abwino mu chirichonse cha iwo. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti ngati Yesu atabwera, ilo lidzakhala gulu-lotulutsidwa. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti ife tiri kutali kwambiri ndi Kubwera kwa Ambuye, monga momwe mpingo ukukhudzidwira, zikhalidwe zathu siziri mu zikhalidwe za Kubwera kwa Ambuye. Ife timalephera nkomwe kukhala nacho chikhulupiriro cha machiritso Auzimu, ngakhale kuti tikwatulidwe. Payenera pachitike chinachake.

36 Bwanji, ngati winawake ayankhula za Mkwatulo, iwo amati, "Kodi iwe ukuyankhula za chiyani?" Ena a anthuwo, mamembala a mpingo. Ukakamba za machiritso Auzimu, "Ine sindimakhulupirira mu zoterozo." Iwo sangakhoze kuwona. Amati, "Chabwino, ine ndikukhulupirira iwo anawapepetula iwo." Chabwino, munthu ameneyo angakhoze bwanji kupita mu Mkwatulo? Kodi iye angawuke bwanji kwa akufa pamene palibe chinthu choti awukemo? Palibe chinthu mmenemo chimene chingamuwukitse iye.

37 Ndi basi kudzipangitsa kukhulupirira, kuwerenga maganizo. Pamene iwe unena kuti, "Ine ndikukhulupirira kuti Yesu Khristu ndi Mwana wa Mulungu," izo ziri bwino, koma, m'bale, ngati izo sizikuchokera mu mtima, bwanji, ndi mwakuganiza basi. Ndipo izo sizingakhoze kubwera kuchokera mu mtima mpaka Mzimu Woyera utachitira umboni za izo. Yesu anati palibe munthu . . . Kapena, Baibulo linati, "Palibe munthu

angakhoze kunena kuti Yesu ndi Khristu, kokha mwa Mzimu Woyera.” Ndipo inu simungakhoze kuzinena izo mwa inu nokha, Mzimu Woyera uyenera kuziyankhula izo kuchokera mwa inu. Yang’anani pamene Yesu . . .

38 Pamene Petro anamuvomereza Iye, iye anati, “Inu ndinu Khristu, Mwana wa Mulungu wamoyo.” Iye anati, “Wodala ndiwe, Simoni Baryona, pakuti thupi ndi mwazi sizinaululire izi kwa iwe, koma Atate Anga amene ali Kumwamba. Ndipo Ine ndikuti, iwe ndiwe Petro, ndipo pa thanthwe ili Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga, ndipo zipata za gehena sizidzawulaka Iwo.” Kodi izo si kulondola? Kotero, inu mukuona pamene ife tiri.

39 Tsopano pakati, tsopano tikufuna tiyambe. Pachiyambi, Mulungu akuitana pansi ndipo anaitana atuluke anthu Ake.

40 Kodi ine ndikuyankhula mokweza kwambiri, M’bale Cox, kapena osati mokweza mokwanira? Mokweza kwambiri pang’ono, ine ndikupepesa ine . . . Chinthu ichi chiri ndi liwu loyipa, ndipo ine ndakhala ndikuzolowera nyumba zazikulu zakale ndi zipinda zoyankhuliramo, ndi panja ndi zinthu, ndipo ine ndikuganiza ine ndimakuwa mokweza kwambiri. Ine sindikutanthauza kuti ndizikalipira pa inu.

41 Tsopano mu Genesis, mutu wa 12, ife tikuyamba woyamba wathu, usikuuno.

> *Tsopano* Ambuye *anali atanena kwa Abram, Choka iwe mu dziko lako, ndi kuchokera kwa abale ako, ndi ku nyumba ya atate ako, upite mdziko limene Ine* ndidzakusonyeza *iwe:*
>
> *Ndipo Ine ndidzakupanga iwe fuko lalikulu, ndipo ine ndidzawadalitsa* iwo amene akudalitsa *iwe, ndipo* Ine ndidza*kulitsa dzina lako; ndipo iwe* udza*khala mdalitso:*
>
> *Ndipo Ine ndidzadalitsa iwo amene akudalitsa iwe, ndipo* ndidza*temberera iye* wakutemberera *iwe: ndipo mwa iwe mabanja onse* a *dziko lapansi adzadalitsidwa.*

42 Abrahamu, akubwera kuchokera ku Babeloni, ndi atate ake, kutsika ku Shinara, a—a Shinara, a—chigwa cha Shinara, kumene miyoyo ya ambiri imayenda pambuyo pa kuwonongedwa kwa Babeloni, kapena chisokonezo chinachitika. Bambo ake a Abrahamu, kholo, anatengera Abrahamu ndi okondedwa ake uko ku Shinara. Ndipo dziko lonse ilo, pakati pa anthu onse awo, Mulungu anapeza kukonderedwa ndi mmodzi, munthu mmodzi anapeza kukonderedwa ndi Mulungu, kani.

43 Tsopano ine ndikufuna kuti inu muzindikire, chimenecho ndi chiyambi cha Chikhristu, cha mpingo. Ndipo ine ndikufuna kuti inu muzindikire, izo sizinali chifukwa chakuti Abrahamu

anali munthu wabwino; icho chinali chifukwa Mulungu anamusankha ndipo anamusankha Abrahamu. Sanali Abrahamu kumusankha Mulungu; anali Mulungu kumusankha Abrahamu. Kodi inu mukukhoza kuziwona zimenezo? Ndipo tsopano penyani. Tsopano, monga izo zinali nthawi imeneyo, chomwechonso izo ziri lero. Si inu kusankha Mulungu; ndi Mulungu kukusankhani inu.

44 Tsopano, izi zikhoza kukhala zamphamvu kwambiri, ndipo ine ndikufuna kuti inu muzindikire. Mwamsanga pakangochitika kusankhako, kusankhidwa, pamakhala kulekanitsidwa kwa china chirichonse, mwamsanga pamene Iye ayitana. Iye amasankha, amaitana. Ndiye pamene Iye wayitana, Iye amakulekanitsani inu ku chirichonse chimene chapachikidwa kwa inu. Izo zimatsimikizira kuti icho si chipembedzo. Si anthu awiri kapena atatu pamodzi. Iye amayembekezera munthu aliyense! Ameni. Ndi chomuchitika cha munthu aliyense payekha.

45 Si chifukwa chakuti amayi anga pamenepo anapulumutsidwa, kuti potero ndine wopulumutsidwa. Ndi chifukwa chakuti Mulungu anandisankha ine, mwa Khristu. Ine ndikufuna inu muchiwone chimenecho. Osati inu kudzisankha nokha; osati kusankha kwanu, kuchuluka kwa momwe inu munapempherera, pamene inu munatsegula tsamba latsopano. Inu munalibe kanthu kochita nazo izo. Mulungu! Oh, mai, pamene inu mufika powona chimene chiri Choonadi! Inu mukuti, "Inu mukutanthauza kuti—kuti ine—ine sindinatembenukire kwa Ambuye?" Ayi, bwana. Iwe unalibe njira nkomwe yotembenukira kwa Ambuye. Chikhalidwe chako chonse, mapangidwe ako onse anali otsutsana ndi Mulungu. Mulungu anakuitana iwe. Izo nthawizonse zakhala zikuchitika mwanjira imeneyo.

46 Mmunda wa Edeni pamene munthu anachimwa, poyamba, tayang'ana chikhalidwe cha wochimwa, akubisala. Koma ankayenera kukhala Adamu kuti azimuyitana Mulungu; anali Adamu akubisala, ndipo Mulungu akumuyitana Adamu. Inu mukuziwona zimenezo? Ndicho chikhalidwe cha wochimwa, kubisala, kuthawa, kupita kuseri kwa chinachake. Koma, Mulungu akuitana! Oh, mai. Chisomo, chisomo chodabwitsa, Mulungu akuitana.

Ndipo tsopano zindikirani, inu mukuti, "Oh, ameneyo anali Adamu ndi Eva."

47 Izo nthawizonse, kudutsa mu Baibulo, chimodzimodzi. Yesu anati, "Palibe munthu angakhoze kubwera kwa Ine kupatula Atate Anga atamukoka iye." Nkulondola uko? Tsopano, amenewo ndi Mawu. Ndipo umo ndi momwe timazifunira izo, Mawu, ndiye iwe umadziwa pamene waima.

48 Ndi angati muno ali ndi . . . ali Akhristu usikuuno, akudziwa kuti ndinu Akhristu, pali chinachake mwa inu chimene chimati ndinu Mkhristu? Inde. Chabwino. Inu mukuona? Bwanji, inu muyenera kukhala anthu osangalala kwambiri padziko lapansi. Inu muyenera kungokhulupirira zimenezo. Mai, ndizo zophweka, muziwatenga Mawu a Mulungu pa izo!

49 Tsopano, inu musanakhale Mkhristu, Mulungu anakuitanani inu. Osati inu kumuitana Mulungu; Mulungu anakuitanani inu. Tsopano, Iye anamuyitana Abrahamu, ndipo iye ndi atate wa ife tonsefe, chikhulupiriro. Zindikirani tsopano, Iye anati, "Abrahamu!"

50 Tsopano, ndi chisankho. Ine ndikufuna kuti ndilowe pa chisankho chimenecho, mwamphamvu, chifukwa ndi Choonadi. Tsopano, inu simunati—inu simunakhale Mkhristu mwangozi, chifukwa, inu munakhala Mkhristu inu musanabwere mu dziko lino. Inu musanabadwe, Mulungu anakudzodzani inu kuti mudzakhale Mkhristu, kuyambira mmunda wa Edeni, kuchokera asanaikidwe maziko a dziko lapansi. "Oh," inu mukuti, "nkulondola uko, m'bale?" Ndicho Choonadi. Mulungu . . . inu musanadziwe nkomwe chirichonse.

51 Inalipo nthawi yomwe inu munkadziwa, anu—malingaliro anu anadetsedwa kwa zimenezo tsopano. Pali Munthu mmodzi yekha pa dziko lapansi amene ankadziwa kuti Iye analipo kale, ndipo ameneyo anali Yesu. Iye anati, "Ndilemekezeni Ine, Atate, ndi ulemelero umene Ine ndinali nawo ndi Inu asanaikidwe maziko a dziko lapansi." Iye anali Mulungu mthupi, Iye amakhoza kusunthira mmbuyo umo ndi kudziwa chomwe icho chinali. Koma malingaliro athu samadziwa za kumeneko.

52 Koma ife tinadzozedweratu, kukonzedweratu. Inu mukudziwa chomwe *kukonzedweratu* kumatanthauza? "Kopita kwa chirichonse, Mulungu anaziwoneratu." Ameni. Umenewo si mkaka wopanda mafuta tsopano. Zindikirani. Ine ndikukhulupirira izo zakupunthwitsani inu. Ife kulibwino tipite kumeneko miniti yokha. Tembenuzirani ndi ine ku Aefeso, mutu wa 1, ndipo tiyeni tiwerenge pang'ono chabe, chifukwa ine ndikuwopa inu—inu mukuchiphonya chimenecho, ndi kungoganiza kuti—kuti ine ndikunena zimenezo. Ine sindikutero. Mvetserani mwatcheru tsopano. Ife tifika ku Mpingo mu mphindi pang'ono, kapena pakapita kanthawi. Tsopano, Paulo akuyankhula, akuyankhula, Aefeso 1, molunjika pa phewa, kwa mpingo. Ndi zomwe ife tikuchita usikuuno. Izi si za makanda. Izi ndi za akuluakulu, osati za makanda.

53 Ana aang'ono, ine ndiri naye mmodzi wamng'ono kumbuyo uko yemwe wangophunzira kumene kuyenda. Iye "amaphunthwa" ndi kugwa pansi, nkudzukanso, ndipo iye amaganiza akuchita chinachake chopambana. Ine ndinali

monga chomwecho tsiku lina; koma tsopano ndine bambo, ine ndinasiya zinthu zachibwana.

54 Tsopano ife tiyenera kubwera ku Chiphunzitso chathunthu. Ine ndimakonda misonkhano yabwino yakale yofuula, kumene ife timangowomba mmanja, kapena kufuula ndi kukhala ndi nthawi yabwino, kukhala ndi mautumiki amphamvu kwambiri ndi zinthu, kuvina pa thovu, monga izo zinkakhalira. Koma, dikirani, ndiye pamene nthawi ya chiwonetsero ifika, iwe sumadziwa pamene iwe waima. Tiyeni tibwerere mmbuyo ndipo tikapeze. Tiyeni tipeze chimene chikutipangitsa ife kuchita izo. Tiyeni tibwerere ku maziko, tikawone pamene ife tiri.

> *Paulo, mtumwi wa Yesu Khristu mwa chifuniro cha Mulungu*. . . (Ine ndimangozikonda zimenezo). . . Palibe seminare yomwe inanditumiza ine kumeneko; *chifuniro cha Mulungu kwa* iwo *amene ali ku Aefeso,* . . . (Tsopano penyani, iye akuyankhula kwa iwo). . . *kwa okhulupirika mwa* Yesu Khristu:

55 Penyani, kuyankhula iwo molunjika kwa ndani? Osati kwa ochimwa, osati kwa makanda, koma kwa iwo amene ali akutha usinkhu.

> *Paulo, mtumwi wa Khristu Yesu mwa chifuniro cha Mulungu,* . . .
>
> Taonani, *chisomo chikhale* kwa *inu, ndi mtendere wochokera kwa Mulungu Atate, ndi kuchokera kwa Ambuye Yesu Khristu.*
>
> *Wodala akhale Mulungu ndi Atate wa Ambuye wathu Yesu Khristu, yemwe* wati*dalitsa ife ndi* mdalitso *wonse wauzimu mmalo ammwambamwamba mwa Khristu* Yesu:

56 Oh, mai! Mwaona yemwe iye akuwayankhula? Osati gulu la makanda. Kwa anthu amene anakhala mmalo Ammwambamwamba, ndipo adalitsidwa. Tsopano iye anati, "Iwe ukudziwa chinachake, iwe unaphunzitsidwa, ndipo iwe unapulumutsidwa, ndipo ine ndikufuna kuti ndikuuze iwe chimene izo zonse ziri." Oh, ine ndimazikonda zimenezo, sichoncho inu? "Ine ndikufuna ndikayike mapazi anu mmwamba Mmiyamba kanthawi pang'ono, mmalo mokhala omangidwa padziko lapansi." Anati, "Tsopano ine ndikufuna ndikuuzeni inu chifukwa chake. Ine ndikufuna ndikupatseni inu pang'ono, pang'ono—kulimbikitsa pang'ono, chitsitsimutso pang'ono, kukondoweza pang'ono." Ameni. Ine ndimakonda kukondoweza, kumakhala ngati kukukumanga iwe, makamaka pamene inu mukudziwa pamene inu mungakhoze kunena kuti ndi PAKUTI ATERO AMBUYE! "Tsopano ine ndikufuna kuyankhula kwa inu," iye anati, "inu amene mukukhala mmalo Ammwambamwamba mwa Khristu Yesu, atadalitsidwa limodzi ndi madalitso onse auzimu, mphatso za Mulungu

zowonetseredwa, machiritso Auzimu, mauneneri, chirichonse chikuchitika. Tsopano ndinu anthu okula usinkhu, ine ndikufuna kuyankhula kwa inu. Ine ndikuyankhula izi kwa inu." Tsopano penyani, "Malingana . . ." Ameni. Tsopano ndi izi apa. Ine ndikuyembekeza izo kwenikweni . . . Ine ndizilola izo zilowerere mkati bwino, mwabwino kwenikweni, chifukwa izo zichita bwino, izo mwinamwake zidzapita mpaka mu mafupa.

*Monga iye anatisankha ife mwa iye . . .*

57 Ndani anatero? "Ine ndinamva izo ndipo ndinabwera"? Ayi, ayi, inu simunatero. "Iye anatisankha, ana (nthawi yakale), anatisankha ife (Mpingo) mwa Iye." Litilo limenelo, Paulo? Sabata yatha, kapena pamene inu munachita chitsitsimutso? Ayi.

*. . . asanaikidwe maziko a dziko lapansi, . . .*

58 Tsopano inu mukhoza kukwera pa mtambo, mwaona. Iye anachita chiyani? "Iye anatisankha ife mwa Iye (Khristu) asanaikidwe maziko a dziko lapansi."

59 Ndikanakonda ife tikanakhala ndi nthawi pang'ono kuti ndipite ku Yobu 7:37, ndi kukawona pamenepo pamene iye anati, "Unali kuti iwe pamene ine ndinkayika maziko a dziko lapansi? Ine ndisanaike maziko a dziko lapansi! Ndidziwitse Ine pamene iwo anamangidwa. Kapena, unali kuti iwe pamene nyenyezi za mmawa zinali kuyimba pamodzi ndi ana a Mulungu ankafuula mwa chimwemwe?" Akumuuza Yobu, "Dzimangire wekha, ngati mwamuna, ine ndikufuna ndiyankhule ndi iwe."

60 Tsopano Paulo akuti, "Iye anatisankha ife mwa Iye, Mpingo, asanaikidwe maziko a dziko lapansi." Tsopano penyani.

*. . . kuti ife tikhale tiri oyera . . .*

61 Osati chiyero chathu chomwe. "Chabwino," inu mukuti, "kodi inu mumakhulupirira mu chiyero, M'bale Branham?" Zedi. Osati changa; mwa Chake. Chiyero changa si kanthu; Chake ndi changwiro.

62 Chabwino, inu mukuti ndiye, "Kodi inu mukukhulupirira kuti inu mukhoza kumwa kapena . . .?" Ayi, ine sindinanene konse zimenezo. Penyani, njere ya tirigu ikhoza kokha kubala tirigu, iyo siyingakhoze kubala chisoso. Mulibemo chikhumbo mwa izo, mulibemo moyo mwa izo kuti ubereke chisoso. Ndipo ngati ife tiri mwa Khristu Yesu . . .

63 Musanyengedwe, inu kulibwino mufufuze izi mwatcheru tsopano. Onani, ngati inu mupitiriza kumati, "Chabwino, ine—ine sizimanditsutsa ine kuchita *izi*, ndipo sizimanditsutsa ine kuchita *izo*," zinthu za mdziko. Tsopano ine—ine ndikupwetekani inu pang'ono pokha, kokerani nthengazo mmbuyo mbali inayo. Koma ndi umboni umodzi uwu wotsimikizika, inu simunakhalepo kwa Khristu. Inu simunayambe mwabadwa mwatsopano.

64 "Iye amene akonda dziko lapansi kapena zinthu za mdziko, chikondi cha Mulungu sichiri nkomwe mwa iye."

65 Tsopano, ngati inu mutangosiya kuchita zimenezo chifukwa inu mukudziwa kuti muyenera kuchita izo, ndi kusiya kuchita *izi*, ndicho chizindikiro kuti inu simunafike paliponse. Pamene chinthu chimenecho chikhala chakufa, mwa inu, ndipo chikhalidwe cha icho nkupita, pamakhala Munthu wina mmenemo ndipo Iye akhoza kungobala. . .Mzimu Woyera umene unali mwa Khristu, mwa inu, umabala Moyo wonga wa Khristu. Palibe chimene inu mumachita; chimene Iye anachita. Iye anasankha zimenezo asanaikidwe maziko a dziko lapansi.

66 Winawake anati, "Chabwino, ine ndikudziwa ine ndinapulumutsidwa, chifukwa ine ndinasiya kusuta."

67 Icho sichinali chifukwa chimene ine ndinapulumutsidwira, icho sichinali chifukwa chimene inu munapulumutsidwira. Inu munapulumutsidwa chifukwa Mulungu anakusankhani inu asanaikidwe maziko a dziko lapansi, kuti mudzapulumutsidwe. Ndicho chiphunzitso cha Lemba. Ameni. Tsopano, inu mukuona, ife tikuyamba kupeza kuti si ifeyo. Ndi Iyeyo, mwaona, Iye anatisankha ife.

68 Abrahamu sakanakhoza kunena kuti, "Chabwino, alemekezeke Mulungu, ine ndinabwera kuno kuchokera ku nsanja ya Babelo. Aleluya! Ndi chifukwa chake ine ndinapulumutsidwa." Iye akanakhoza kupulumutsa gulu lonselo ndiye, ngati ndicho chifukwa chimene iwo anachitira zimenezo. Mwaona, Iye sanachite zimenezo.

69 Iye anamusankha Abrahamu. Ndipo chimenecho chinali chiyambi chomwe cha chipulumutso chathu chimene chinaperekedwa kwa munthu, pamene Iye anamuyitana iye, ndipo anamusankha iye, ndipo anamukonzeratu iye, ndipo anamupatsa iye lonjezo, ndipo anapanga pangano ndi Abrahamu ndi Mbewu yake, kwanthawizonse. Tsopano ife tikhoza kupita patsogolo apa ndi kukawerenga mutu wathunthu mu zimenezo, koma ife tiribe nthawi. Tsopano, Mulungu anayitana. Penyani, pamene Iye anamuyitana Abrahamu apa, Iye anamuyitana iye mwa kusankha. Osati chifukwa *iye* anali; chifukwa *Mulungu* anali. Ndipo Iye anamuyitana iye kuti achoke kwa anthu ake, ndipo anamudalitsa iye, ndipo anamuuza iye kuti "Ine ndikupulumutsa iwe." Ndipo mpaka pansi apa, Iye akuti, "Ndipo iwe udzabwera kwa Ine mu m'badwo wokhwima wakale." Iye asanachite chirichonse choti chimuyenereze icho, Mulungu anamusankha iye, anamuuza iye. "Ndipo osati iwe wekha, komanso Mbewu ya pambuyo pako." Oh, mai! Zindikirani. "Ndipo iye anabwerera. . . " Ndime ya 8. Tsopano tiyeni tiwerenge mpaka pansi apa patsogolo pang'ono pa chinthu china ichi.

> *Kotero* Abrahamu *anachoka, monga* A*MBUYE* *anali atayankhulira kwa iye; ndipo Loti anapita ndi iye: ndipo Abramu anali wa zaka sevente ndi faivi zakubadwa pamene iye anaturuka ku Harani.*
>
> *Ndipo Abramu anamutenga Sarai mkazi wake, ndi Loti mwana wa mchimwene wake, ndi chuma chawo chonse*. . .

70 Tsopano penyani, iye anachita apo pomwe chimene Mulungu anamuuza iye kuti asachite, iye anamutenga Loti mdzukulu wake, ndipo Abrahamu anawatenga abambo ake. Koma Iye sanamuuze iye kuti awatenge abambo ake, koma iye anawatenga iwo, mulimonse. Ndipo wowerenga Baibulo aliyense, inu mudzawerenge izi mu Genesis mawa pamene mudzakhale ndi nthawi. Zindikirani kuti inali ntchentche mu mafutawo, mpaka munthu wachikulireyo anamwalira. Iye anali chopunthwitsa njira yonseyo, ndipo chomwechonso anali Loti. Mulungu anamuyitana Abrahamu, osati Loti. Iye anamuyitana Abrahamu, osati abambo ake.

71 Chabwino, inu mukuti, "Nanga bwanji Sarah?" Mwamuna ndi mkazi wake ndi mmodzi. Aefeso, "Iwo ali thupi limodzi," Baibulo linanena chomwecho. Chabwino.

72 Koma Iye anamuitana Abrahamu ndipo anamufunsa iye, ndipo anamuuza iye kuti adzilekanitse yekha ku zonse zomwe iye anali nazo, ndi kubwera mdziko lachirendo.

73 Taonani, kulekanitsidwa! Ndikupita mdziko lachirendo limene iwe sukudziwa kalikonse za ilo, ndicho Chikhristu. Kudzilekanitsa ku zinthu za mdziko, chifukwa Mulungu wakuitana iwe. Kupita ku dziko lina, kukakhala pakati pa anthu omwe iwe sukudziwa kalikonse kawo, kuti ukakhale mwendamnjira. Ameni. Pamene ine ndiganiza za zimenezo, ine sindingakhoze basi kudzigwira ndekha. Mwendamnjira! Mlendo!

74 Yakobo wokalamba, pakufa, atayima pamaso pa Farao, iye anati, "Ine ndakhala ndiri zaka *zambiri* mu umwendamnjira wanga." Ameni. Kodi iye anali chiyani? Iye anayamba kubwera kwa iyemwini. Mwana wamng'onoyo anali atachita moyipa kwambiri. Iye ankadziwa kuti iye anangokhala mwendamnjira kuno. Tsopano zindikirani.

75 Ife tikufika mpaka mmusi ku ndime ya 8, ndipo Mulungu akumulonjeza Abrahamu apa momwe Iye ati amupulumutsire iye ndi Mbewu yake pambuyo pake. Tsopano, Iye anapanga pangano, lopanda mangawa. Izo siziri chimodzimodzi basi kuti Iye anazipanga izo basi chifukwa chakuti iye anali—kuti iye anali Abrahamu. Iye sananene kuti, "Tsopano, Abrahamu, ngati iwe uti uchite *izi*, ngati iwe uti uchite *izo*." Iye anati, "Abrahamu, ine ndachita kale izo. Icho si chinthu chimene iwe uyenera kuchita. Ine ndazichita izo, Inemwini!" Ameni. Oh, mai, pamene

ine ndiganiza za zimenezo! Mulungu anachita izo, Iyemwini, mopanda mangawa. Pangano la Mulungu ndi lopanda mangawa!

76 Inu mukuti, "Chabwino, m'bale, ine ndinasiya kudya nyama. Ine sindimachita *izi*. Ine . . . " M'bale, izo ziribe chinthu chimodzi chochita ndi zimenezo. Si ngati inu mumadya nyama kapena simudya nyama, kapena kusunga masiku a Sabata kapena mwezi watsopano, kapena kaya inu mumapita ku Sande sukulu Lamlungu, kapena chimene *ichi* chiri. Inu munapulumutsidwa, mopanda mangawa!

77 Ndiye inu mukuti, "M'bale Branham, ndiye ngati ine ndapulumutsidwa, ulemelero kwa Mulungu, ine ndikhoza kuchita chimene ine ndikufuna kuchita." Inde, bwana. Ndipo ngati inu mwapulumutsidwa, m'bale, iwe sumakhala ndi chikhumbo cha chirichonse cha mdziko. Ndipo mtima wako wonse umakhazikika pa Icho, iwe sungakhoze kudzipatula kwa Icho. Koma bola ngati pali kukoka pamenepo, iwe umadziwa kuti pali cholakwika apobe.

78 Tsopano, kusankhidwa, Mulungu anamuyitana Abrahamu, anamuuza iye kuti Iye akanati amupulumutse iye, mopanda mangawa.

79 Tsopano tiyeni tipite cha apa lonjezo litatha kanthawi pang'ono. Ine ndikufuna inu mupite nane ku Genesis 15:7, apa mphindi yokha, ndipo tiyeni tiwerenge apa kwa mphindi pang'ono chabe. Chabwino.

> *Ndipo* Ambuye *anati kwa iye, Ine ndine* Ambuye *amene ndinakutulutsa iwe kuchokera ku Uri wa*. . . Akaldia, ndipo *ndinapereka* kwa *iwe dziko ili likhale cholowa chako.*
>
> *Ndipo iye anati, Ambuye MULUNGU,* ndidzadziwa *bwanji kuti ilo lidzakhala cholowa changa?*

80 Tsopano, Abrahamu, atatuluka mdzikolo, Akaldia, dziko, mzinda wa Uri wa Akaldia, dziko la Shinara, wolekanitsidwa, anatuluka. Taonani zimenezo, chimodzimodzi monga Akhristu lero, akungoyendayenda. Penyani.

> *Ndipo iye anati kwa iye, Nditengere ine ng'ombe yaikazi ya zaka zitatu, ndi mbuzi yaikazi ya zaka zitatu, ndi nkhosa ya mphongo ya zaka zitatu, ndi njiwa, ndi nkhunda.*

81 Tsopano, mawa ine ndikufuna inu kuti mupitirire ndi kukawerenga izo, ngati inu mukuzilemba izo, mpaka mmusi. Ine ndizibwereza izo, chifukwa cha nthawi, danga, chifukwa ine sindikufuna kuti ndikusungeni inu nthawi yaitali. Ine ndikufuna inu mudzabwerenso mawa usiku, kotero ife tikhoze kudzalowa mu izi. Ife tikungoyika a—maziko usikuuno, maziko chabe. Mukuona?

82 Ndipo iye anatenga izi, ng'ombe yaikazi, mbuzi yaikazi, ndi nkhosa yamphongo, ndi ziwiri...njiwa ndi nkhunda, ndipo anagawaniza nkhosa yamphongo ndi ng'ombe, ndi zina zotero, ndipo anaziyala izo. Kuyika njiwa mmenemo, ndi popanda...popanda kuyigawa iyo. Ndipo anasunga mbalame kuzichotsa pa izo zisachokepo mpaka dzuwa litalowa. Ndipo Mulungu anatsikira pa Abrahamu, kudzatsimikizira pangano limenelo, anabwera uko, anati, "Tsopano, Abrahamu, tsopano Ine nditsimikizira kwa iwe chimene Ine ndikufuna kuti ndichite." Ndipo Iye...

83 Ndipo inu mukudziwa, ambiri a inu anthu munali muno mu mpingo, zaka zapitazo, ine ndinaphunzitsa chinthu chomwechi. Inde. Inde, bwana. Mmbuyo mu 1949 ine ndinali kuphunzitsa zimenezo. Chabwino, iye anali atazilemba izo mu Baibulo lake.

84 Taonani! Ndiye Iye anabwera pansi ndipo anadzasonyeza kwa Abrahamu chimene Iye anali kupitako. Poyamba, Iye anamuika Abrahamu kuti agone, "Tsopano, Abrahamu, iwe ulibe kanthu kochita ndi izo."

85 Tsopano, kwa inu amene mukuyesetsa kuti mudzipulumutse nokha. Ine ndamva kuti mu tchalitchi, mkachisi, titatha kukhala pansi pa Kuphunzitsa kumeneko, kuti anthu ambiri anachoka mu kachisi, anatuluka kukalowa mu miyambo ndi zina zotero, ku—kukakhulupirira mitundu yonse ya chirichonse chimene chiripo kuti chikhulupiriridwe. Anasiya, ena a iwo asiya kudya nyama, ndipo ena a iwo akusunga masiku awo a Sabata ndi mwezi watsopano, ndipo sindikuti...Ine ndikuganiza akuchita zansembe, ndi chirichonse, atatha kukana kwenikweni kuvomereza Mawu a Mulungu. Izo zikusonyeza chomwe icho chinali umu. Paulo anati, "Iwo anatuluka chifukwa iwo sanali a ife." Mwaona, ndiko kulondola. Mwaona, izo nzoona. Mzimu Woyera umagwira Mawu a Mulungu. Zinthu zimenezo, pa chiwonetsero, zidzatsimikiziridwa kuti iwo akulakwitsa.

86 Tsopano, Iye anati, "Abrahamu." Iye anamugonetsa iye tulo, anati, "Ine ndikusonyeza iwe momwe Ine nditi ndichitire izo, momwe Ine ndisungire pangano Langa." Ndipo Iye anatenga nyama zimenezo, ndipo tsopano penyani, pamene Abrahamu anakagona tulo, kusonyeza kuti imfa iyenera kubwera kwa cholengedwa chirichonse. Ndiye ng'anjo yoyaka moto inapita patsogolo pake; ndipo ng'anjo yoyaka moto inkaimira gehena, kuti wochimwa aliyense ayenera adzapite ku gehena. Ndiyeno kupitirira izo, mwa nsembe pa phiri, panapita Kuwala koyera pang'ono, kumene kunapita pakati pa chirichonse cha zidutswa za nsembezo. Pangano!

87 Ngati mungazindikire, pakhala pali njira zambiri zomwe anthu amapangira pangano, nthawi zambiri. Ife lero, timapanga bwanji pangano? Titi, "Chanza, ndipatseni ine faivi." Umenewo ndi mgwirizano. Ndiro pangano lathu, sichoncho? Mmasiku

akale, iwo ankakonda ku-. . . Ku China, inu mukudziwa momwe iwo ankapangira pangano? Iwo amaponyerana mchere wina ndi mzake. Limenelo ndi pangano ku China. Mwaona, ndipo iwo amapanga mapangano osiyanasiyana, miyambo ya anthu yosiyanasiyana.

88 Koma mwambo wakummawa unali kupha chinyama, ndi kudzayima pakati pa chinyama ichi, ndiyeno nkuzilemba. Cha apa inu mukuzipeza izo, mu Levitiko, ndipo iwo amalemba apa mgwirizano wawo. Ndipo mgwirizano umenewo umang'ambidwa pawiri, pa chinyama chakufa ichi. Ndipo iwo amalumbirira pa chinyama chakufacho, kuti, ngati iwo aswa pangano ili, mulole thupi lawo likhale ngati chinyama chakufa ichi. Ndipo amampatsa aliyense chidutswa. Ndiyeno iwo amatumizidwa azipita. Ndipo pamene abwerera, zidutswa ziwiri zimenezo zimayenera kulumikizana ndendende basi zidutswa zomwezo. Ndi zokongola bwanji!

89 Mulungu akupanga pangano, kusonyeza, kuwonetseratu kuti "Ine ndalumbira kuti Ine ndidzachita zimenezo, mu Mbewu yako Ine ndidzadalitsa mafuko onse a dziko lapansi." Kawerengeni zimenezo. "Ine ndidzadalitsa Amitundu, Ine ndidzadalitsa munthu wakuda, wachikasu, munthu woyera. Ine ndidzadalitsa aliyense kudzera mu Mbewu yako, pakuti kuchokera mwa iwe kudzabwera mafumu ndi akalonga."

"Inu mudzachita motani izo, Ambuye?"

"Ine ndidzakusonyeza iwe kuti ndi motani."

90 Ndipo Iye anakamusonyeza iye kumbali kwa phiri, kumene zidutswa zimenezo zinaimiridwa. Ndipo wophunzira Baibulo aliyense pano akudziwa kuti iliyonse ya izo inali nyama yoyera zimenezo zinkaimira Nsembe ya Yesu Khristu. Iye anali Mwanawankhosa. Iye anali Ng'ombe yaikazi yomwe inkapanga madzi olekanitsa pamene munkadutsa mmadzi olekanitsa. Tsopano ife tikumakhala ndi kutsukidwa ndi madzi, mwa Mawu olekanitsa ku tchimo, kudzera mu Mawu, kudzera mu kukhulupirira. Ndipo Nkhunda ndi Njiwa, zinali machiritso Auzimu, izo zonse mwa Khristu! Ameni.

91 Pamenepo Mulungu anamuwonetsa Abramu zomwe Iye akanati achite, kuti kudzera mwa Mbewu ya Isaki Iye akanadzabala Mwana Wake wobadwa yekha, Khristu, ndipo anaphedwa kutaliko pakati pa thambo ndi dziko lapansi, pamene dzuwa linkalowa, mdima pa dziko lapansi, ndipo pamenepo Iye anamung'amba Iye pakati. Mulungu anatulutsa Solo Yake mwa Iye, ndipo Iye analemba pangano ndi mabanja a dziko lapansi. Pamene Mwazi wamtengo wapatali uja wosaipitsidwa wa Mulungu Wamphamvuzonse, ukuwukha kuchokera mu Mitsempha ya Emanuele, Iye anang'amba Solo imeneyo kuchoka mwa Iye. Iye anati, "Mulungu Wanga, Mulungu Wanga, ndi chifukwa chiyani Inu mwandisiya

Ine?" Nkhope Yake yodzaza ndi malovu achipongwe, chisoti chachifumu chamnyozo chinakokedwera pa mphumi Pake, misomali Yake inakhomeredwa, zinali zinsonga za Chiroma, nsana Wake unang'ambika mpaka nthiti Zake zinkawonekera, akulendewera pa mtanda, akufuula, kufa imfa ya wochimwa, tchimo la dziko lapansi pa Iye. Ndipo pamenepo Mulungu anang'amba mbali Zake, anang'amba Solo Yake kuchoka mwa Iye, pamene Iye anati, "Mmanja Mwanu Ine ndikuwupereka Mzimu Wanga," ndipo Iye anagwetsa mutu Wake. Ndipo dziko lapansi linagwedezeka ndi kugeya miyala yake. Ndi Uyo pamenepo, ndi limenelo pangano la Mulungu! Ndi kumeneko kukwaniritsidwa kwa zimenezo.

Pakati pa miyala yosweka ndi mmlengalenga mwakuda
Mpulumutsi wanga anaweramitsa mutu Wake ndipo anafa,
Chophimba chotsegula chinawulula njira
Ku zisangalalo za Kumwamba ndi tsiku losatha.

92 Oh Kalvare, Oh Kalvare, Yesu anakhetsa magazi ndipo anandifera ine! Ndiye Iye anang'amba Solo ya Mwana Wake Yemwe, analekanitsa pangano, ndipo Iye anaponyera thupi mnthaka. Ilo linagona mmenemo kwa masiku atatu usana ndi usiku. Ilo linawuka! "Pakuti sikunali kotheka kuti Woyera Wanga Uyo adzawone chivundi, kapena kuti Ine sindidzasiya Solo Yake mu gehena." Ndipo Solo Yake inali Mzimu Wake umene unatsikira ku gehena. Ndipo Iye anauka pansi, Mulungu anatero, ndipo anatenga thupi Lake ndipo anamupatsa Iye moyo, ndipo anatenga thupi la Yesu ndipo anakaliyika ilo pa dzanja Lake lamanja mu Ulemelero, ndipo anatumizanso Mzimu Woyera ngati Pangano.

93 Ndi zimenezotu. Musati muphonye pa izo, m'bale. Popanda ubatizo wa Mzimu Woyera, inu mwatayika. Ndicho chokhacho . . . Inu simusowa kudandaula za kupita Kumwamba. Ngati mulibe kalikonse *muno* Chauzimu, zitseko sizingakhoze kutsegulidwa, inu mukhoza kuyenda pamenepo ndi kumenyetsa mutu wanu pa icho. Koma ngati Mzimu wa Mulungu uli mmenemo, Mzimu wa Mulungu mkatimo udzatsegula zitseko. Muyenera kukhala nacho chinthu *muno* kuti chikatsegule icho kumeneko. Ndiko kulondola. Kotero inu munaweruzidwa kale pa zomwe inu mumaganiza za Yesu Khristu.

94 Tsopano, apa Iye akubwera, wong'ambika, wamasanza, wong'ambika mu zidutswa. Solo Yake inapita kwa Mulungu. Mulungu anamudalitsa Iye. Ndiyeno Solo Yake inabwereranso mu mawonekedwe a ubatizo wa Mzimu Woyera umene umabwera mwa wokhulupirira aliyense, kudzayeretsa, kuyeretsa malingaliro, kuyeretsa mtima, ndi kudzasiya gawo la Mzimu Woyera mmenemo, apa ndi apo. Ndipo pamene

Mzimu Woyera uperekedwa, Mzimu Woyera womwewo umene unatulutsa thupi la Yesu kuchokera mmanda, Udzakwatula. Ndipo pangano limenelo liyenera kulumikizana, monga Iye anang'ambira pamenepo ndipo napereka thupi; anabwerera kwa Mulungu, ndipo Mzimu unadzabwerera pa dziko lapansi. Ndiye Mzimu wanu uyenera kudzakhala Mzimu wa mtundu womwewo, kapena iwo udzaphonya malo aja opita limodzi. Ameni. Inde, bwana. Osati chifukwa inu mumadzipanga nokha, koma chifukwa Chinachake, chikondi cha Mulungu chasesa kulowa mu solo yanu, chimene chang'amba fano lirilonse la padziko lapansi. Ndi zimenezotu.

95 Ndipo pali chinachake chimene chimangopuma ndi kuyitanira kwa Mulungu, ndi solo yanu umu ikuitanira kwa Atate Akumwamba. Ndi zimenezotu. Zimenezo zimakupatsani inu chikhulupiriro, ndipo inu mumadzakhala Mbewu ya Abrahamu. Inu mumakhulupirira lonjezo la Mulungu monga Abrahamu anachitira. Ngakhale ilo litachedwa, komabe inu mukulikhulupirira ilo. Mokhulupirika! Abrahamu sanazandime pa lonjezo la Mulungu, mwa kusakhulupirira, koma anali wamphamvu, akupereka matamando kwa Mulungu.

96 Ndipo inu simungakhale opulumutsidwa kuchokera ku chitsitsimutso chimodzi kupita ku chimzake. Ndiye nkumadzitcha nokha Mbewu ya Abrahamu? Inu kulibwino muganizire chinachake poyamba. Musaweruze molakwika chirichonse. Khalani molunjika ndi Mawu.

97 Abrahamu sanagwedezeke pa lonjezo la Mulungu, kudzera mu kusakhulupirira. Pamene Iye anamuuza iye kuti Iye akanadzamupatsa iye mwana wamwamuna, iye anadikirira zaka twente-faivi, amakhala wamphamvu nthawi zonse. Iye ankakula mu chisomo ndi chidziwitso cha Ambuye. Ameni.

98 Sindinalinge kuti ndifike pa kulalikira, koma Izo zinangoyamba kulalikira mwa ine. Chabwino.

99 Mulungu akuitana, akusankha. Tsopano, inu mukhoza kukumanizana nazo izo, alipo anthu omwe sadzapulumutsidwa konse. Pali anthu omwe sadzapulumutsidwa konse, ziribe kanthu zomwe iwo akuchita. Ndipo inu mukudziwa zimenezo. Pali anthu omwe anakonzedweratu kuti adzatayika. Pali anthu amene anakonzedweratu kuti adzapulumutsidwa. Onse amene anakonzedweratu kuti adzapulumutsidwa, adzapulumutsidwa, mulimonsemo.

100 Zimenezo, zimenezo sizinapite bwino. Izo zikuwoneka ngati simunazimvetse izo. Chabwino, tiyeni titembenuzire apa, tiyeni tingozipeza izo ndiye, tiwone chimene Mulungu ananena. Tiyeni tifike, tiyeni tifike mu Chipangano Chatsopano poyamba. Ndipatseni ine Aroma 9, miniti yokha, ndipo ife tiwona ngati izi ziri zoona kapena ayi, tiwone ngati Mulungu ananena kuti ena adzatayika, ndipo ena omwe—omwe akanati adzakhale.

Kodi mumawakonda Mawu a Mulungu? Chabwino, tiyeni tiwone chimene Iwo akunena tsopano. Tsopano mvetserani mwatcheru. Tengani nthawi yanu, musakhale pa liwiro. Tsopano penyani Aroma 9, Paulo akuyankhula, Chipangano Chatsopano. Ndakutengerani malo ambiri mu Chakale.

101 Ndipo inu amene mukulemba, lembaninso Yuda 4, pamene inu muli pamenepo, "Amuna akale, okonzedweratu ku kutsutsidwa uku, anthu akusandutsa chisomo cha Mulungu kukhala chonyansa, kutuluka kukatsatira zilakolako za chidziko." Umo mu Timoteo aponso, pamene Iwo amati, "Monga Yambre ndi Yane anatsutsana ndi Mose ndi Aroni, momwemonso awa adzatsutsa Choonadi; amuna amalingaliro otayika." Mulungu anati iwo adzakhala pamenepo, ndipo iwo ali pano!

102 Tayang'anani pa zinthu zabodza. Inu mupite kunja kuno, mupite kudutsa mmipingo ya Chipentekoste, Amethodisti, Abaptisti, Achiyero, kulikonse kumene inu mukufuna kutero, inu mukawapeza anthu akutsanzira Icho, anthu akudzipanga ngati kuti ndi iwowo. "Chabwino, ulemelero kwa Mulungu. Aleluya!"

103 Mkazi ananena tsiku lina, "Ine ndiri nawo ana teni, koma, ulemelero kwa Mulungu, Ambuye anandiitana ine kuti ndidzalalikire Uthenga. Aleluya, ine ndikupita kunja, ndikachite izo." Iye sanachite chinthu choterocho. Iye sanatero ndipo Iye sadzatero konse, chifukwa Iye anati Iye sadzatero. Tsopano, koma, oh, mai, iye ankaganiza chomwecho. Inde, bwana. Mulungu anamupatsa iye ana teni kuti awalere, ndicho chimene iye ankayenera kuchita. Chabwino. Koma chinthu chake ndi chakuti, iwo amadzikweza okha pansi pa kutengeka.

104 Chabwino, iwo amanena kuti, "Ine sindikusowa aliyense kuti andiphunzitse ine. Ulemelero kwa Mulungu, ine ndiri nawo Mzimu Woyera." Chabwino, ndiye, Mzimu Woyera unalakwitsa pamene Iwo unati Iwo unawaika ena mu mpingo, aphunzitsi? Mulungu anawaika iwo mu mpingo, monga aphunzitsi. Izo zikukhazikitsa izo. Ndi chifukwa chiyani Iye anayika aphunzitsi mmenemo, ngati Mzimu Woyera uti udzachite kuphunzitsa konseko? Mukuona? Chabwino. Mukuona?

105 Chimene anthu akusowa ndi kubatizidwa kwa ubongo wawo, pambali pa madzi awo. Uko nkulondola. Chabwino. Ndikhululukireni kuyankhula kwakuthwa kumeneko, koma ine—ine ndimakonda kuzilola izo kuti zilowelere mkati. Ife tikufuna chitsitsimutso, ndipo, m'bale, inu muyenera kuchikondoweza chinthucho. Inu musanachite izo, inu muyenera kumutenga Satana akankhidwire kutali. Musamakangane naye iye, muzitenga malo anu ndi kuyima pamenepo. Ndinachita kumenyana naye iye, kuzungulira dziko lapansi, ndipo Mkhristu wina aliyense yemwe anayamba

wamuimirirapo Mulungu ayenera kumenyana naye iye. Koma ngati iwe ukudziwa chimene waimamo, chimene ukudziwa kuti ndi Choonadi, ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE, iwe ukhoza kuyima pamenepo.

106 Inu mukuti, "Chabwino, ulemelero kwa Mulungu, ine ndinapulumutsidwa chifukwa ine ndinasiya kumwa. Ulemelero kwa Mulungu, ine ndinali ndi tsemwe linatsikira ku nsana kwanga. Ine ndinali ndi mphepo yamkokomo, yamphamvu inandigunda ine ku nkhope. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo, M'bale Branham?" Ndithudi. Koma ine ndikufuna ndiwone kumene mphepo, ya mkokomo yamphamvu imeneyo inachokerako, poyamba. Mukuona? Izo nzoona. Zoonadi. Limenelo ndi tsemwe, chabwino, koma ine sindinapulumutsidwe chifukwa ine ndinali ndi tsemwe, ndipo osati chifukwa ine ndinali ndi mkokomo, mphepo yamphamvu. "Inu simumakhulupirira mu zimenezo, m'bale?" Inde, ine ndimatero. Koma dikirani miniti, tiyeni tibwerere apa pang'ono pokha. Mdierekezi ali nazo zabodza zina cha pamenepo.

107 Ine ndinapulumutsidwa chifukwa ine ndinakumana ndi zikhalidwe za Mulungu. Iye anandiyitana ine, ndipo ine ndinadziwa kuti Iye wandiyitana ine. Ine ndinamulandira Iye pa Mawu Ake, chotero ine ndikhoza kumuuza Satana, "PAKUTI ATERO AMBUYE!"

108 Pamene Yesu anali kuno pa dziko lapansi, Iye anali Mulungu, Iye anali Emanuele. Mulungu anali mwa Khristu, akuliyanjanitsa dziko kwa Iyemwini. Iye sanagwiritse ntchito iliyonse ya mphatso Zake zazikulu, pamene Iye anakomana ndi Satana. Iye anati, "Kwalembedwa, 'Munthu sadzakhala moyo ndi mkate wokha.' Kwalembedwa, 'Iwe usamuyese Ambuye Mulungu wako.'" Iye anamugonjetsa iye. Ndi zimenezotu, kudziwa Lemba. Satana amalidziwa Ilo, nayenso, koma iwe umayenera kudziwa momwe ungawagawire molondola Mawu a Mulungu. Mukuona?

109 Zindikirani, mvetserani kwa Paulo akuyankhula. Ndi angati angavomereze Chiphunzitso cha Paulo? Iye anati, "Ngati Mngelo adzaphunzitsa china chirichonse, musiyeni iye akhale wotembereredwa."

> *Ine ndimanena choonadi mwa Khristu, ine sindimanama, chikumbumtima changanso* chikuchitira *umboni mwa Mzimu Woyera,*

110 Mvetserani kwa Paulo akudzitsimikizira yekha, mwaona, kuziyika izo kuti inu mwamtheradi mudziwe.

> *Kuti ine ndiri nacho chisangalalo chachikulu ndipo* icho. . .*chisoni mu mtima mwanga.*
>
> *Pakuti ine ndikanakhoza,* ine. . .*Pakuti ine ndikanafuna kuti inemwini ndikhale wotembereredwa*

*kwa Khristu kwa abale anga, achibale anga monga mwa thupi:*

111 Inu munamvapo akuti, "Oh, Ayuda onse ndi anthu osankhidwa a Mulungu." Izo si zoona. Izo si zoona. Ayuda si anthu osankhidwa ndi Mulungu. Mwaona, iwo siali. Tsopano mvetserani, muwone ngati Paulo sananene chinthu chomwecho, ndipo iye anali Myuda. Mwaona, Abrahamu anali ndi ana amuna eleveni. Inu mukudziwa zimenezo, sichoncho inu? Ndipo iwo onse anali mbewu ya Abrahamu. Iwo onse anali Mbewu ya Abrahamu, koma "Mwa Isaki Mbewu yako idzaitanidwa." Osati mwa ena onsewo, osati mwa Ishmaeli, ndipo osati mwa ana aamuna naini ochokera kwa winayo, mkazi wachitatu yemwe iye anali naye. Ayi. Izo zinali, "Mwa Isaki munali Mbewu itaitanidwa." Dikirani, ine ndikukhulupirira kuti izi ziri mmutu womwewo.

*Amene* anali *Aisraeli; kwa amene kukhazikitsa umwana, ndi ulemelero, ndi* pangano, *ndi kupereka kwa lamulo, ndi utumiki wa Mulungu, ndi malonjezo;*

112 Tsopano, iye akuyankhula za Israeli tsopano. Tsopano mpenyeni iye, zomwe iye akunena.

*Amene ali a atate, ndi a* iwo amene ali okhudzi-. . . chifukwa cha *thupi Khristu* adzabwera, *amene ali pamwamba pa zonse, Mulungu alemekezeke kwa nthawi zonse. Ameni.*

*Osati ngati kuti mawu a Mulungu. . .sanagwire ntchito. Pakuti iwo sali onse Israeli, amene ali. . . Israeli:*

113 Nkulondola kumeneko? Ndiye si onse ali Israeli amene ali a Ayuda kumeneko, iwo si onse a iwo. Penyani.

*Ngakhale, chifukwa iwo ndi mbewu ya Abrahamu, . . .*

114 Izo sizimawapanga iwo kukhala a Israeli. Tsopano penyani. "Kodi inu mukufanizira chiyani, M'bale Branham?" Ine ndikufanizira Mpingo. Onse amene amavomereza Khristu si Akhristu. Onse amene amapita ku tchalitchi si Akhristu. Mbewu yonse ya Abrahamu sanali Khri-. . .sanali, amene anali ndi lonjezo. Iwo anali osankhidwa, ilo linali lonjezo. Ndipo lonjezo linanenedweratu kwa Abrahamu. Ndipo osankhidwa a Mulungu anakonzedweratu asanaikidwe maziko a dziko lapansi. Mukuona? Zindikirani!

*Komanso osati, chifukwa iwo ali mbewu ya Abrahamu, iwo ali ana: koma, Mwa Isaki mbewu yako idzaitanidwa.*

115 Osati mwa Ayuda ena onse, koma mwa Isaki. Kupyolera mwa Isaki kukubwera Khristu. Imeneyo inali Mbewu ya Abrahamu, ndiyo Khristu. Ndiyeno Mbewu ya Abrahamu, choyamba, sinali kupyolera mu mbewu ya kugonana, chinali chikhulupiriro

chake chimene Mulungu anachiwerengera. Ndi kupyolera mu chikhulupiriro, mwa ife, kukhulupirira imfa, kuikidwa mmanda, ndi chiukitsiro cha Khristu, zikutibweretsera ife, Mbewu ya Abrahamu.

116 Ndipo Abrahamu analandira mdulidwe, monga chisindikizo cha lonjezo ku chikhulupiriro chake. Tsopano, iye sanalandire ilo pamene iye anadulidwa, iye analandira lonjezo iye asanadulidwe.

117 Ndi kulondola uko, eledara? [M'bale akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Ali kuti M'bale . . . ? mlaliki winayo, ine ndinamuwona iye atakhala, Ine ndikuganiza iye akujambula kumbuyo uko, M'bale . . . Inde. Chabwino.

118 Iye analandira lonjezo iye asanadulidwe. Aroma 4 adzakuuzani inu. Iye analandira lonjezo iye asanadulidwe. Kenako iye anapatsidwa mdulidwe monga chisindikizo cha kumvera kwake kwa chikhulupiriro. Tsopano pamene ife tinena kuti . . . Ndi chifukwa chake Billy Graham, Charles Fuller, ndi Billings ndi onse amenewo, chifukwa chimene iwo akuyankhula za, abale awo Achibaptisti. Ine ndinawauza ambiri a iwo chomwecho, Rufus Mosley ndi gulu lonselo. Ine ndinati . . .

119 Iye anati, "Chabwino, ife tinali nawo otembenuka twente sauzande mu masabata awiri. Iwo sanakawapeze anthu twente."

Ine ndinati, "Iwo sanatembenuke."

"Oh," iye anati, "iwo anamulandira Khristu ngati Mpulumutsi wawo."

120 Ine ndinati, "Komabe, iwo sanatembenuke." Uko nkulondola. Iwe sumatembenuka mpaka . . . *Kutembenuka* kumatanthauza "kusinthidwa." Ndipo taonani, Paulo . . .

121 Petro anali atakhulupirira pa Ambuye, iye anali atabatizidwa, anapatsidwa mphamvu yochiritsa odwala, kutulutsa ziwanda, kuwukitsa akufa. Ndipo Yesu anamuuza iye, usiku wa kupachikidwa kusanachitike, "Iwe ukadzatembenuka mtima, udzamulimbikitse m'bale wako." Nkulondola uko? Anali atapulumutsidwa ndi kuyeretsedwa, ndipo anali asanatembenuke. Ndiro Lemba.

"Oh, kodi iye anayeretsedwa?" Inde, bwana!

122 Yohane 17:17, "Ayeretseni iwo, Atate, kupyolera mu Choonadi." Inu mukuganiza kuti Iye akanayika Mzimu umenewo mu chotengera chimene sichinali choyenera? Ndipo iwo anapita kunja uko ndipo anakatulutsa ziwanda; ankabwerera, akufuula. Chabwino, Amethodisti. Iwo ankabwera, akufuula, akulemekeza Mulungu, ndipo anati, "Oh, ziwanda zimatimvera ife!"

123 Oop, kamphindi chabe! Mateyu 10, ndipo Iye anati, "Musakondwere chifukwa ziwanda zimakumverani inu, koma

mukondwere chifukwa maina anu analembedwa Kumwamba.” Ndi kulondola uko?

124 Tsopano ine ndikufuna ndikutontholetseni inu miniti yokha. Ndipo Yudasi anali ndi iwo. Ndi kulondola uko? Yudasi anali ngati bakha wamkulu momwe anali mu dziwe. Iye anali akufuula ndi kusangalala, nayenso. Ndipo iye anawutsatira mpingo mpaka mmusi mpaka iwo unafika ku Pentekoste. Koma pamene iwo unafika ku Pentekoste, kuti udzalandire ubatizo wa Mzimu Woyera, iye anawukana Iwo, ndipo anamupereka Yesu. Ndipo ameneyo anali wotsutsakhristu. Ndipo mzimu umenewo lero udzabwera pansi pomwe ndi kudzaphunzitsa kulungamitsidwa mwa chikhulupiriro, ndi chirichonse, ndi kudzasunthira mpaka mmusi ku ubatizo wa Mzimu Woyera, ndiyeno nkudzasonyeza mitundu yake. Ndizo ndendende.

125 Ndipo penyani anamwali teni amene anatuluka. Faivi. . . Onse a iwo anamwali. Faivi a iwo anali opusa; faivi anali ndi Mafuta mu nyali zawo. Kodi Mafuta ndi Chiyani? Mzimu Woyera. Mukuona? Uko nkulondola. Iwo one anali anamwali, ankakhala moyo wabwino, miyoyo yoyera.

126 Inu mukuti, “Chabwino, m’bale, ine sindimapita ku zovina, ine sindimapita ku ziwonetsero.” Icho ndi chinthu cha makhalidwe basi. Pokhapokha ngati patachitika Chauzimu! Osati chifukwa inu munafuula, osati chifukwa inu munayankhula ndi malirime, osati chifukwa inu munalumpha mmwamba ndi pansi, osati chifukwa inu munachita *izi*; koma chinachake Chauzimu chachitika mkati *umu*, chimene chakusinthani inu ndi kuyika. . .Inu munasindikizidwira kutali mwa Mulungu. Inu mwazikika. Uko nkulondola.

127 “Chabwino, inu simukukhulupirira?” Ine ndimakhulupirira mu kufuula, ine ndimakhulupirira mu zinthu zonse izi, koma ilo sindiro Yankho.

128 Amethodisti ankaganiza, pamene iwo anafuula, iwo anali nawo Iwo, koma iwo anapeza kuti iwo amalakwitsa. Ambiri a iwo anafuula, ndipo analibe Iwo. Apentekoste anadzabwera pamenepo, iwo anadzayankhula mmalirime, iwo anati “ife tamupeza iye,” koma iwo anapeza kuti amalakwitsa. Ambiri a iwo anayankhula mmalirime, analibe kalikonse. “Ngakhale ndingayankhule ndi lirime la anthu ndi a Angelo, ndipo ndiribe chikondi, izo sizindipindulira ine kanthu.” Iwo analibe Iwo. Uko nkulondola. Ndipo ndicho chifukwa chake dziko lonse linanyengedwa ndi zimenezo, ndi kupyolera mu chinthu chinacho. Limenelo si Yankholo. Osati chiwonetsero chathupi chirichonse kapena kutengeka, koma chinachake chachitika mkati *umu* chimene chinasintha malingaliro anu onse, chinasintha chikhalidwe chanu chonse. Inu mwatembenuzidwa; osati inuyo, koma Khristu wabwera mwa inu ndipo wadzakutembenuzani inu. Chikhalidwe chanu

chafa, mwa munthu wakale, ndipo inu mwabadwa kachiwiri, ndipo ndinu munthu watsopano. Penyani. Ameni.

129 Mukuti, ine ndikuchedwa pano, sichoncho ine? Mundifuulire ine pang'ono pokha, kumbuyo uko, abale, ngati nditi nditalikitse pang'ono kwambiri. Ine ndiyenera kuti ndiwatenge ana a Israeli kumusi kuno, mu miniti yokha, koma ine ndikufuna ndikuwonetseni inu momwe iyi iliri ntchito ya Mulungu kuti azichita zinthu izi. Inu mukundikondabe ine? Chabwino. Tsopano pitirirani kundipempherera ine. Chabwino. Koma mungondilola ine ndiziziziritse pang'ono chabe ndiye, tsopano, mphindi chabe.

> *Komanso osati, chifukwa chakuti iwo ndi mbewu ya Abrahamu, iwo ali ana: koma, Mwa Isaki mbewu yako idzaitanidwa.*
>
> *Kuti* izo *ziri, Iwo amene ali a—ana athupi,* amenewo *siali ana a Mulungu: koma ana a lonjezo* (oh, tayang'anani pamenepo) *akuwerengedwa ngati mbewu.*

130 "Ana a lonjezo." Analonjeza chiyani? Ndi lonjezo la mtundu wanji? Limene Mulungu analonjeza asanaikidwe maziko a dziko lapansi. Iye anawaitana iwo. Ndiyo Mbewu. Osati chifukwa inu munasiya kuchita *izi* ndipo munasiya kuchita *izo*, ndipo munasiya kunama, munasiya kuba. Zimenezo ndi machitidwe amakhalidwe basi, mzika yabwino imachita zimenezo. Inu simungakhoze kudzitcha nokha Mkhristu, apobe, mpaka chinachake mkati *umu* chitachitika, mpaka inu mutasinthidwanso, chinachake chimene chachitika mkati *umu*. Zindikirani.

> *Pakuti awa ndi mawu a lonjezo,* Monga *nthawi iyi* Ine ndidza*bwera, ndipo Sarah* adzabala *mwana wamwamuna.*
>
> *Ndipo osati ichi chokha; koma pamene Rebeka nayenso anali ndi pakati pa mmodzi,* (mvetserani kwa ichi tsopano), *ngakhale mwa atate wathu Isaki;*

131 Valani jekete lanu, konzekerani chisoti chanu. Ichi chikutembenuzani inu.

> *(Pakuti anawo pokhala asanabadwe,* (uyu ndi Esau ndi Yakobo) *komanso asanachite . . . chabwino kapena choipa, kuti cholinga cha Mulungu monga mwa kusankha . . .*

132 Ine ndikuzilola izo zilowerere kwa nthawi yaitali. Dzukani tsopano, pang'ono chabe. "Esau ndi Yakobo, mwana aliyenseyo asanabadwe, iwo asanadziwe ngakhale chimene chinali chabwino ndi choyipa."

> . . . kuti *kusankha* kwa Mulungu *kukhoze kuyima, osati kwa ntchito, koma kwa iye amene ayitana;)*

133 Psyii! Ine ndimaganiza kuti umasiya kudya nyama kuti upulumuke? Iwe ulibe kanthu kochita ndi zimenezo! Ngati unapulumutsidwa, Mulungu anakuitana iwe asanaikidwe maziko a dziko lapansi, ndipo anakupulumutsa iwe. Ndi kulondola uko? Tsopano penyani.

> Monga kunalembedwa, monga *izo* ziri *kunenedwa* kwa *iye, Wamkulu adzatumikira wamng'ono*.

> *Monga kunalembedwa, Yakobo Ine ndamukonda,* ndipo *Esau Ine ndinamuda*.

134 Mwana aliyenseyo asanabadwe, Mulungu anati, "Ine ndamukonda mmodzi ndipo ndadana naye winayo." Kodi amenewo ndi Mawu a Mulungu? Ine ndiribe choyankhira pa Iwo, palibe china koma kuwalalikira Iwo.

135 Tsopano, kusankha si kanthu komwe inu mumayenera kuchitapo; ndi chimene Mulungu anachita. Mulungu anachita izo mwa Khristu, kwa inu, asanaikidwe maziko a dziko lapansi. "Onse amene Atate andipatsa Ine adzabwera kwa Ine." Aleluya! Oh, mai! Mundikhululukire ine. Sikuti ine ndatengeka; koma ndine wokondwa. "Onse amene Atate andipatsa Ine adzabwera kwa Ine, ndipo iye amene abwera kwa Ine sindidzamtaya konse kunja. Iye amene adya Thupi Langa ndi kumwa Magazi Anga, moyenera, iye atalandira Mzimu, ali nawo Moyo wosatha. Ine ndidzamuukitsa iye tsiku lomaliza." [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi].

136 Iwe ukuopa chiyani? Huh! Mulungu analonjeza, mopanda mangawa. Chikondi icho cha Mulungu chikuyimba mu mtima mwanu, ndipo inu mukudziwa kuti inu mwadutsa kuchokera ku imfa mwapita ku Moyo, inu mumamukonda aliyense, ndipo a—dziko lonse lakhala losinthika kwa inu, ndipo iye wazikika pamenepo ndipo palibe chomwe chimakusunthani inu, ingokhalani okondwa ndi kumapitirira. Ulemelero kwa Mulungu! Musalole kanthu kakutembenuzireni inu mopotoloka. Oh, inu mukhoza kutuluka panja ndi kukazizidwa ndi kukagwedezeka pang'ono pokha, koma Mbewu ya Mulungu imeneyo ikhalabe yoona. Baibulo linati, "Ngakhale ife sitikhulupirira, komabe Iye sangakhoze. Iye ndi woona, Iye amaima mokhulupirika." Tsopano penyani. Tiyeni tiwerenge.

> *Kodi ife tidzatani* ndiye, *kodi ife tidzanena chiyani ndiye?* (Mvetserani kwa Paulo) *Kodi kulipo kusalungama* mwa *Mulungu? Mulungu aletse*. Kodi kulipo kusalungama?

> *Pakuti iye anati* kwa *Mose, Ine ndidzachitira chifundo pa amene Ine ndimchitira chifundo,. . .Ine ndidzamchitira chifundo pa amene ine ndidzamchitire chifundo*.

> *Kotero ndiye* ngati *sikuli kwa iye amene afuna,. . .*

137 Oh, inu mukuti, “Ulemelero kwa Mulungu, aleluya, ine ndidzapulumutsidwa ine ndisanafe.” Inu mukutero? Mulungu ali ndi chinachake choti anene za izo.

> . . .osati *iye amene* afuna (ayi, choncho), *kapena . . . iye amene athamanga,* (chiyani?) *koma kwa Mulungu amene* asonyeza *chifundo.*

138 Si iye amene athamanga kapena iye amene afuna, ndi Mulungu amene amasonyeza chifundo. Ndi kusankha kwa Mulungu. Mulungu amachita zimene Iye akufuna.

139 Tsopano zindikirani patsogolo pang’ono chabe. Ine ndazilemba zimenezo apa ndi zilembo zofiira, mochuluka kwambiri, zonse zitaphimbidwa mpaka ine ndikulephera kuziwona izo. Izo, ndi zomwe ine ndaziwerenga Izo mochuluka kwambiri muno. “Za ku . . . ” Ine sindikudziwa chomwe izo ziri pamenepo, ndi a . . . inde, zafufutidwapo. Ine ndikuwona kuti izo ziri apa, ine ndazifufuta izo zonse ndi inki yofiira pamenepo. “Lembalo . . . ” Ine ndikatenga Baibulo langa lina mawa usiku.

> . . .amene *anena . . . Farao, Ngakhale kwa* awa, *cholinga chomwechi ine ndamuukitsa* iye, *kuti ine ndikakhoze* kusonyeza *mphamvu yanga mwa inu, ndi kuti dzina langa lilalikidwe* kwa onse, *pa dziko lonse lapansi.*

140 Mulungu anamuukitsa Farao, ndipo anawumitsa mtima wake, kwa cholinga chimenecho. Mulungu anamuukitsa Yudasi Iskarioti, iye anabadwa kuno mwana wa chitayiko. Ndi kulondola uko? Mulungu anauza Esau ndi Yakobo, iwo asanabadwe nkomwe, anawauza amayi ake zonse zimene zikanati zidzachitike, mmodzi amene Iye ankamuda ndi wina amene Iye ankamukonda. Kodi izo nzoona? Kotero ndi Mulungu Amene amachita zinthu zonse mu zinthu zonse, ndipo inu mulibe chochita nazo izo. Ndipo ngati Mulungu wakuyitanani inu, chikondi cha Mulungu chikuyimba mu mtima mwanu. Ndipo onse amene Iye wawayitana adzabwera kwa Iye, ndipo palibe mmodzi wa iwo adzatayike. Mulungu analonjeza, Iye anati, “Palibe mmodzi wa iwo amene adzatayike. Onse amene Atate andipatsa Ine, adzabwera kwa Ine. Ndipo palibe mmodzi wa iwo wotayika koma Yudasi Iskarioti, kuti Malemba akakhoze kukwaniritsidwa. Ndipo Ine ndidzawawukitsa iwo pa tsiku lotsiriza.”

141 Tsopano inu muli, inu munanena kanthawi kapitako, kuti ndinu Mkhristu. Nchiyani chinakupangani inu kukhala Mkhristu? Chifukwa Mulungu anakuitanani inu asanaikidwe maziko a dziko lapansi, kuti mudzakhale Mkhristu, ndipo inu munadzakhala Mkhristu. Zitatero inu munapulumutsidwa, munadzazidwa ndi Mzimu Woyera, inu muli nawo Moyo Wamuyaya. Nchifukwa chiyani Iye anakupatsani inu Mzimu

Woyera? Monga Chisindikizo cha chikhulupiriro chanu. Inu munali ndi chikhulupiriro poyamba.

142 Tsopano, ngati inu mukuti, "Chabwino kodi...? Inu munanena kanthawi kapitako za Billy Graham ndi iwo akufuula, 'Ndani onse...Ndi angati akufuna kumulandira Khristu ngati Mpulumutsi wawo. Akweze mmwamba dzanja lawo.' Kodi izo ziri bwino?" Ndithudi, izo zonse nzabwino. Izi ndi zabwino, koma icho ndi chiyambi chabe. Ndiye ngati inu mukukhulupirira izo kwenikweni ndipo mwalandira izo mu mtima mwanu, ndipo mwaphunzitsidwa molondola, ndiye Mzimu Woyera udzabwera ngati mdulidwe, umene Iye anamupatsa Abrahamu mwa chikhulupiriro chake, chitsimikiziro.

143 Tsopano inu mukuti, anthu amati, "Tiyeni tikhale ndi msonkhano wodikirira. Ulemelero kwa Mulungu, tiyeni tibwerere mmbuyo." Ndipo kuti, "Ulemelero kwa Mulungu, tiyeni tiyembekezere Mzimu Woyera." Palibe chinthu choterocho.

144 *Tarry* sizikutanthauza "kupemphera." *Tarry* amatanthauza "kudikirira." Ndi angati akudziwa kuti mawu akuti *tarry* amatanthauza "kudikirira"? Yesu anati, "Mukadikirire uko mu mzinda wa Yerusalemu mpaka ine...mpaka lonjezo litaperekedwa kwa inu." Ine sindikudziwa chimene iwo anali kuchita. Iwo mwinamwake anali kupemphera. Ine sindikudziwa.

145 Koma iwo sankayenera kuti azidikirira zitachitika zimenezo. "Pamene Petro anali chiyankhulire Mawu awa, Mzimu Woyera unagwera pa iwo." Pansi ponse! Ndipo pamene Paulo anaika manja ake pa iwo, Mzimu Woyera unabwera pa iwo. Ndi kulondola uko? Mwaona, palibe kudikirira. Mzimu Woyera unali pamenepo ndipo unawapatsa iwo ubatizo wa Mzimu Woyera, potsimikizira chikhulupiriro chawo.

146 Ndipo Mulungu anampatsa mdulidwe Abrahamu, potsimikizira chikhulupiriro chake. Ndipo icho chinali chiyani? Kodi Mzimu Woyera ndi chiyani? Winawake andiuze ine kuti Mzimu Woyera ndi wachiyani. Ndi chizindikiro. Ndi kulondola uko? Kodi mdulidwe unali wa chiyani? Chizindikiro. Ndi kulondola uko? Chizindikiro. Mulungu anapereka chizindikiro kuti Iye anali atamulandira Abrahamu, kwa mdulidwe.

147 Ndipo pamene inu munena kuti, "Ine ndimakhulupirira Mulungu, ine ndimakhulupirira Yesu Khristu," ndiye Mulungu amakupatsani inu ubatizo wa Mzimu Woyera, ngati chizindikiro kuti Iye wavomereza chikhulupiriro chanu. Aleluya! Ndipo zikatero inu mwasindikizidwa mu Ufumu wa Mulungu; osati mpaka chitsitsimutso china, koma mpaka tsiku la chiwombolo chanu. Aefeso 4:30, "Musawukwiyitse Mzimu Woyera wa Mulungu umene inu munasindikizidwa nawo mpaka tsiku la chiwombolo chanu." Ndi zimenezotu.

148 Tsopano mwamsanga, pafupifupi utali wa maminiti faivi, tiyeni tipite ku Genesis 45. Ndipo ine ndikufuna kuti ndikatenge chi—chidule chaching'ono chodabwitsa apa, kuti ndiwabweretse ana a Israeli awa mpaka kumalo kumene inu mudzawatenge iwo mawa usiku ndi kuwatulutsa iwo. Ine ndikupepesa kuti ndachedwerapo pang'ono usikuuno, koma ine ndimayenera kuti ndiyambe izi poyamba.

149 Tsopano, Abrahamu analandira lonjezo. Isaki anabwera motsatira. Inu mukudziwa nsembezo. Ine ndayesetsa kuti ndikubwezereni inu, kuti mpingo umenewo kumbuyo uko ukuitanidwa utuluke, kusankha, unali wa Mulungu, chimodzimodzi monga momwe izo ziliri lero. Iye anamuyitana Abrahamu mwa kusankha; Iye akuwuitana mpingo mwa kusankha. Iye anamupatsa Abrahamu lonjezo, Abrahamu anakhulupirira ilo; ndipo Iye akuwuitana mpingo lero. Inu mukumukhulupirira Yesu Khristu? Ndiye, choyamba, inu mukhulupirire. Ndiyeno Mulungu anali ndi Abrahamu ndi ana ake, mbewu yake, wodulidwa mdulidwe ngati chizindikiro; ndipo Iye amakupatsani inu Mzimu Woyera lero ngati chizindikiro.

150 Kodi Mzimu Woyera ndi chiyani lero, kwa munthu, pamene Iwo ubwera? Ndiwo mdulidwe. Kodi—kodi Stefano sananene chomwecho, mu—mu Machitidwe, mutu wa 7? pamene iye anati, "Oh, inu osadulidwa mu mtima ndi mmakutu, inu nthawizonse mumakaniza Mzimu Woyera. Monga makolo anu anachitira, momwemonso mukuchita inu." Ndi kulondola uko? Ndipo Mzimu Woyera ndi mdulidwe. Ndipo kodi mdulidwe umachita chiyani? Umadula mnofu wosefukira, zinthu zonse za mdziko. Iwo umakudulani inu kuti mutalikirane nazo zinthu za mdziko, chikondi cha mdziko, chikondi cha thupi, kunyada kwa moyo. Iwo umangokudulani inu kwa izo. Inu mulibe kanthu kochita nazo izo; Iwo umachita izo Wokha, ndipo umakuikani inu mu chikondi ndi Yesu Khristu, ndi chikondi chosafa. "Palibe chimene chingakulekanitseni inu ku chikondi cha Mulungu chimene chiri mwa Khristu Yesu." Paulo anati, "Zowopsya ndi mayesero, ndi ndende, ndi china chirichonse, palibe chiripo, palibe mtsogolo, chingakhoze kutilekanitsa ife kwa chikondi cha Mulungu chimene chiri mwa Khristu Yesu."

151 Ndipo Iye anakuitananani inu, anakupatsani inu mdulidwe, anawuika iwo. . . inu mwa Iye, ndipo anakukonzeranitu kopita kwanu Kwamuyaya. Ngati izo siziyenera kuti ziwapangitse Akhristu kufuula, ine sindikudziwa chomwe chingachite izo. Ngati izo sizingamudzutse munthuyo amene—amene ali mwa Khristu, ine sindikudziwa chimene chingatengere kuti chimudzutse iye; ine ndikukhulupirira kuti iye wafa kawiri, wazulidwa ku mizu. Sichoncho inu? Chabwino.

152 Tsopano, ndiye Iye anayitana, kenako Iye anabweretsa Mbewu Yake kumeneko. Chinthu chotsatira, Iye anabwera

kumeneko kudzera mwa Abrahamu, ndipo kenako kudzera mwa Isaki, ndipo kenako kudzera mwa Yakobo, kenako kuchokera kwa Yakobo kupita kwa Yosefe. Tsopano penyani, ngati ife tikanakhala nayo nthawi, nthawiyina, kuti tipite mu izi. Ife tidzatero, koma osati tsopano. Penyani, kusankha ndi mwa Abrahamu. Kodi inu munazindikira? basi mbadwa foro zimenezo, ndiyeno iko kunatha, kunaphwasuka. Kunatuluka mwa mbadwa thwelovuzo ndipo mafukowo anasiyana. Ndi kulondola uko? Ndipo adzatero. . . Sukunabwerere konse kachiwiri mpaka iko kunadzabwerera mwa Imodzi, Mbewu ya Abrahamu; kenako iko kunadzabwera mwa Munthu, yemwe anali Khristu, ngakhale anapatsidwa ulemelero kuno pa dziko lapansi ndipo anakwezedwa mmwamba mwa Mulungu. Ndipo Mzimu Woyera unabwereranso kudzafalitsa mmafuko onse, kudzalizadzitsa dziko lapansi ndi chidziwitso cha Ambuye, mwakuya ngati Mmiyamba, ndipo, oh, umenewo ndi Mzimu Woyera lero.

153 Tsopano penyani. Kusankhidwa, mwa Abrahamu; kulungamitsidwa, mwa Isaki; chisomo, mwa Yakobo; ndi ungwiro, mwa Yosefe. Palibe chinthu chimodzi chimene chinalembedwa motsutsa Yosefe. Umenewo ndi ungwiro. Masiteji atatu apa dziko lapansi a umwendamnjira wa ana a Israeli, ndipo chachinai chinali pamene iwo anapita mdziko lolonjezedwa, lomwe linali Zakachikwi. Ndi masiteji atatu a mpingo wa Amitundu. Sabata ino, Mulungu pokhala wololela, ine ndikhoza kuzibweretsa izo kudutsa mu Baibulo ndi kukuwonetsani inu kuti ife tiri mu siteji yathu yachitatu, tsopano wokonzeka kupita mu Zakachikwi mu nthawi ya Yosefe.

154 Tsopano penyani, pamene chirichonse chinawunjikana mwa Yosefe. Chiyani? Munthu wangwiro; amene anabadwa mwa abambo ake, wokondedwa ndi abambo ake, wodedwa ndi mchimwene wake. Tsopano tayang'anani mofulumira tsopano, chifukwa ine ndiyenera kufulumira, ndipatseni ine chidwi chanu chosagawanika. Wokondedwa ndi Abambo Ake, wodedwa ndi m'bale Wake; Ambuye Yesu, penyani Yesu akuchita mu khalidwe lirilonse mmenemo. Tayang'anani pa Yosefe, wangwiroyo. Oh, ife tikhoza kukhala masabata pa iye. Penyani, wodedwa ndi m'bale wake, wokondedwa ndi atate ake. Chifukwa chiyani? Iye anali munthu wauzimu. Iye ankawona masomphenya, amakhoza kutanthauzira maloto. Iye anali wauzimu. Wachikulire wake wamng'ono. . . abale ake anati, "Zamkhutu! Chokapo."

155 Tsopano taiwonani mipingo lero. Taonani mbali yauzimu. Ambuye Yesu mu mpingo Wake lero, Iye amadedwa ndi mphukira zonse. Mwaona, chimodzimodzi basi. Kusekedwa, kumutcha Iye "wotentheka," konsekonse. Chabwino, izo ziyenera kutero. Apa pali choyimiridwa; apa pali mthunzi wake.

Inu mukuti, "Chabwino, M'bale Branham, ngati ine ndilandira Mzimu Woyera, iwo onse akandiseka ine."

156 Chabwino, ngati inu simunatero, inu simunaulandire Iwo. Inu mukuyenera kudedwa ndi dziko lapansi. Yesu anati, "Iwo amamutcha Mbuye wa nyumbayo 'Belezebule,' ndi mochuluka bwanji momwe iwo ati adzawatche ophunzira Ake, mwaona, iwo a mnyumbamo." Tsopano, Iye anali. Ndipo penyani.

157 Ndiye iye anali wokondedwa. Ndipo bambo ake . . . Chimene, ife sitingasuntheko, kuchoka kwa ichi. Abambo ake anampatsa iye malaya amitundumitundu. Ndi kulondola uko? Tsopano, ngati inu mungawuwone mwinjiro umenewo wopanda msoko, umene unkaimira Mzimu Woyera umene unkaphimba umunthu wake. Ndipo lero ndi Mzimu Woyera umene ukuphimba mpingo, Mwinjiro wa mangamanga. Ndipo pali mitundu seveni mu utawaleza. Mukuona? Ndipo mitundu yake seveni yangwiro ndi mitundu yonse imene ife tiri nayo. Ndipo iwo amalumikizana limodzi kupanga utawaleza. Ndipo utawaleza, mu Baibulo, umatanthauza pangano. Ndipo Mulungu anapanga pangano Lake ndi Nowa, osatinso madzi, koma ndi moto nthawi yotsatira, Iye anampatsa iye chizindikiro cha utawaleza, ndipo ife tikadali nachobe icho. Ndi kulondola uko?

158 Tsopano ngati inu mungatembenuze (ngati ine ndikanakhala nayo nthawi kuti nditenge Malemba ena awa) ku Chivumbulutso, mutu woyamba. Ndipo pamene Yohane anamuwona Iye atayima, "Mmodzi wonga Mwana wa munthu, atayima pakati pa zoyikapo nyali zisanu ndi ziwiri zagolide," zomwe zinali Mibadwo Isanu Ndi Iwiri ya Mpingo.

159 Ndipo ife tinayamba ndi Efeso, ndipo tinakathera ku Laodikaya, m'badwo wofunda wa mpingo kumene ife tiri tsopano, "Okhala nawo mawonekedwe aumulungu, koma kumakana mphamvu yake." Kupita ku tchalitchi, ndi kukhala ndi anthu kuti azibwera ndi kumadzanena kuti "landirani Khristu" ndi kumalemba dzina lawo pa bukhu; koma kumakana ubatizo wa Mzimu Woyera ndi mphamvu, ndi zozizwitsa, ndi zizindikiro, ndi zodabwitsa, kumawuseka Iwo, mu M'badwo wa Mpingo wa Laodikaya, umene unalavulidwa kuchokera mkamwa mwa Mulungu; ndipo Osankhidwa anatengedwera mmwamba. Oh, aleluya! Oh, chinachake chimalowa mmoyo wanga pamene ine ndiganiza za izo, amzanga. Oh, dziko mu chikhalidwe chake lero!

160 Ndipo apo Iye anali, atayima pamenepo. Chiyani? Ndipo Iye anali woti ukamuyang'ana ngati mwala wa Yaspi ndi Sarde. Kodi Yaspi anali chiyani? Kodi Rubeni anali mwala. Kodi Sarde anali chiyani? Benjamin. Woyamba ndi wotsiriza. Iye anali woti ukamuyang'ana monga Woyamba ndi Wotsiriza. Ndi utawaleza kuzungulira mutu Wake, pamwamba pa zoyikapo nyali seveni zagolide. Utawaleza, pangano limene Mulungu

anapanga kudzera mwa Abrahamu, kudzera mwa Isaki, kudzera mwa Khristu, kudzera mu mpingo, mwa ubatizo wa Mzimu Woyera. Mwinjiro wa mitundu seveni umene unali pa Yosefe, umene unali pa Yesu, uli pa mpingo lero, wotetezedwa. Thupi linali litaphimbidwa ndi mwinjiro. Ndipo mpingo si inuyo, ndi Mzimu Woyera umene wakuphimbani inu ndi Magazi, Pangano la Mulungu, lokonzedweratu asanaikidwe maziko a dziko lapansi.

161 Aleluya! Ine ndimangoyenera kuzitulutsa izo. Chabwino. Izo zinali pafupi kuti zindiphulitse ine. Zindikirani, ndiroleni ine ndikuuzeni, inu mukhoza kuganiza kuti ndine wamisala. Ngati ine ndiri, ndine wokondwa, ndisiyeni ine ndekha. Chabwino. Ndiroleni ine ndikuuzeni inu chinachake. Oh, ine ndingakhale bwanji kusakhala wokondwa, ndikudziwa zimene ine ndikuzidziwa? Ine ndingakhoze bwanji kuzigwira izo, ndikudziwa zimene ine ndikuzidziwa? Ine ndikuyesetsa kuti ndizifikitse izo kwa anthu. Mai! Izo zingamupangitse aliyense kukondwa. Psyii! Mai! Chabwino.

162 Apo Iye anali, ndipo Yakobo anali. . .ndipo Yosefe anali choyimira Chake. Chophimba, abambo—abambo anamupatsa iye mwinjiro. Aleluya. Kodi inu simukukumbukira pamene Yesu anabatizidwa, "Anapita molunjika akuchoka mmadzi, ndipo, taonani, miyamba inatseguka kwa Iye, ndipo Mzimu Woyera unatsika monga Nkhunda, ndipo inapita pa Iye, anati, 'Uyu ndiye Mwana Wanga wokondedwa mwa Iyeyu Ine ndikondwera.'" Iye sanachite chozizwitsa kufikira pamenepo. Ndiye mpaka mu chipululu kuti akayesedwe, ndipo mpaka kukachiritsa odwala, ndi mphamvu za Mulungu.

163 Ndiwo mpingo. Pamene iwo wabatizidwa, iwo wavekedwa ndi Mzimu Woyera, ndi mphamvu. Oh, mai!

164 Chochitika chomwecho cha chiberekero cha Sarah kukhala chakufa, Isaki asanabwere. Mulungu anangozisiya izo kuti zipitirire. Iye anali usinkhu wa zaka sikisite pamene iye analandira lonjezo. Iye anali usinkhu wa zaka nainte mbewuyo isanayikidwe konse mwa iye. Mwangwiro, mwamtheradi chodabwitsa!

165 Ndipo munthu yemwe wabadwa mwatsopano, ndi chodabwitsa. Aleluya. Si kulandira, kapena kukweza dzanja lako monga *chonchi*. Ndi mphatso ya Mulungu. Chodabwitsa! Kubadwa mwatsopano, kuchotsedwa mu dziko lino mu dera la zokhudzira. Inde, bwana. Bwanji, chifukwa inu mukuyenera zimenezo? Chifukwa Mulungu analonjeza izo, kuti lonjezo likhoze kukhala lotsimikizika, molingana ndi kusankhidwa.

166 Ndiye Yosefe anagulitsidwa kwa pafupifupi zidutswa sarte za ziliva, ndi m'bale wake. Mpingo wa Chiyuda unamupereka Yosefe.

167 Lero, muli chiyani mu mpingo uno? Kuperekedwa. Iwo akupeza zikalata, iwo ayesetsa kuti akhale ndi a . . . Chabwino, tsopano, inu mungozisunga izi mmalingaliro anu. Iwo akhala ndi chitaganya cha mipingo. Matchalitchi a Khristu aku America achita kale chitaganya ndi mipingo yawo yonse, ndipo iwo adzakhala ndi gulu loyimba kuno tsiku lina limene liti lidzatseke, kuti akamenyere Chikominisi, zomwe zidzalumikizane ndi Chikatolika, ndi mpingo wa Chiprotestanti ndi mpingo wa Katolika limodzi. Ndipo zipembedzo zosakanikirana zomwe zikuyimira Choonadi, ndi kuchokako ku mbalume imene iwo ali nayo, zidzazunzidwa. Chilemba cha chirombo; Chisindikizo cha Mulungu; chiwonetsero chibwera posachedwapa. Ndipo, m'bale, ngati Iwo mulibe *mmenemo*, inu mudzanyengedwa motsimikiza basi monga dziko, chifukwa izo zizidzawoneka zabwino kwambiri. Izo zidzati, "Tsopano, ngati Chikominisi chinapanga a—a—chinapanga a . . . chifukwa cha dziko, bwanji, tiyeni ife tipange mgwirizano wina, ndi kuwabweretsa Akhristu onse, ndi kulipangitsa dziko likhalenso Lachikhristu." Ndipo nkumawoneka zabwino kwambiri, anthu azidzalumphira mmenemo. Mukuona? Iwo adzaichita chitaganya mipingo, ndi kudzaibweretsa, kuyesetsa kudzachipanga Chikhristu kukhala chinthu chimodzi. Ndipo Baibulo limati, mu Chivumbulutso, kuti iye anapereka mphamvu yake ndi chirichonse, kuti iye anapanga fano kwa chirombo ndi kuchita mphamvu zonse zimene chirombo chinachita pamaso pake. Ndithudi, izo ndi choncho. Ndikukhumba ife tikanakhala nayo nthawi kuti ndilumikize Chivumbulutso mu chinthu ichi (koma ife tiribe, mwaona), kuti tiwone pamene izo ziri. Inu muli pomwe pano kumapeto kwa nthawi, m'bale. Ife tiri kumapeto kwa m'badwo.

168 Ndiye iwo anamugulitsa Yosefe, zidutswa sarte za siliva. Anamuponyera iye mu dzenje, kuti iye afe. Iye anatengedwera mmwamba, anatumizidwa mmenemo pamenepo. Ndipo pamene iye anali mu ndende yake kumeneko, iye . . . Panali amuna awiri, woperekera chikho ndi a—ndi a—ndi wophika mkate. Ndipo mmodzi wa iwo anatayika ndipo winayo anapulumutsidwa, ndi Yosefe yemwe anapereka loto ndi kutanthauziridwa.

169 Ndipo chinthu chomwecho pamene Yesu anapachikidwa pa mtanda, panali wakuba mbali imodzi, ndi wakuba mbali inayo, ndipo mmodzi anatayika ndipo winayo anapulumutsidwa. Ndendende basi.

170 Kenako iye anatengedwera pamaso pa Farao, ndipo anakatanthauzira loto, ndipo iye anapangidwa kukhala munthu wa dzanja lamanja la Farao, palibe munthu akanakhoza kumuwona Farao popanda kubwera kwa Yosefe.

171 Ndipo choimira changwiro cha Yesu, atakhala pa dzanja lamanja la Mulungu, ndipo palibe munthu amabwera kwa

Mulungu kupatula kudzera mwa Khristu. Ndendende basi choyimira changwiro pamenepo.

172 Ndipo zindikirani, apa pali chinthu china, inu anthu Amitundu tsopano molingana ndi Mbewu ya Osankhidwa, Yosefe anapatsidwa mkwatibwi wa Amitundu. Iye anakanidwa ndi m'bale wake, ndipo anatembenuka nakatenga mkwatibwi wa Amitundu. Ndi kulondola uko? Iye anampatsa iye, Farao anampatsa iye wansembe wa Or, mwana wamkazi, akhale mkwatibwi. Ndipo iye anakwatira mkazi wa Amitundu, amene anabala Efraimu ndi Manase, amene anali wolowa limodzi mu ufumu, kulowa mu lonjezo la mbadwa.

173 Zindikirani momwe Yesu wangwiro, wokanidwa ndi Ayuda, anatumizanso Mzimu Woyera, ndipo iwo anawaseka iwo nawaseleula iwo, ndipo anati, "Iwo aledzera ndi vinyo watsopano." Ndi kulondola uko?

174 Ndipo Yesu anati, "Inu mukhoza kundichitira Ine mwano, ndi kumapitirira nazo izo; koma ngati mudzayankhula mawu amodzi motsutsa Mzimu Woyera, izo sizidzakhululukidwa konse kwa inu."

175 Ndipo Ayuda amenewo anabwera kumeneko, ndipo anati, "Chabwino, amuna amenewo akhuta vinyo watsopano, ha, ha, ha," ndipo anawaseka iwo. Ndipo osapitirira zaka sarte, kapena mwabwinoko, kuyambira pamenepo, kudzafika pamene Tito anadzazinga makoma ndipo iwo anadyerana ana a wina ndi mzake, ndipo iwo anawapha iwo ndi kutentha kachisi, molingana ndi Mawu a Mulungu. Ndipo iye sanawukitsidwenso konse, kufikira masiku a Amitundu atadzatha. Ndipo kumeneko ine ndikukonzekera kuti ndikacheze ku Yerusalemu mu masabata angapo akubwerawa, ndipo kumeneko mabwinja akale amenewo, ndipo khoma lolira liri kumenekolo. Kumene iwo anamwazikana padziko lonse lapansi, chifukwa Mulungu anawauza iwo kuti iwo akanadzachita izo, ndipo iwo anabwera kumeneko ndi kudzachita izo. Uko nkulondola. Oh, mai! Kuganiza za—themberero la kuwukana Mzimu Woyera! Tsopano, Mzimu Woyera unatsanuliridwa pansi, ndipo iwo anawukana Iwo.

176 Ndipo pamene Ayuda anawukana Iwo, Amitundu anawulandira Iwo, chimene chinali choyimira cha Mkwatibwi. Iye anati Iye adzaitana anthu kuchokera mwa Amitundu, chifukwa cha Dzina Lake.

177 Mtsikana wamng'ono uja wakhala kumbuyo uko, anali Broy, koma iye ndi Branham tsopano, iye ndi mkazi wanga.

178 Ndipo a—Mkwatibwi wa Yesu Khristu adzakhala Akazi a Yesu Khristu (Aleluya!), anabatizidwa mu Mzimu Wake, mu Dzina Lake, odzazidwa ndi mphamvu Yake, anavekedwa chirungamo Chake. Aleluya! Ndi Uyo apo. Ndipo tsopano zindikirani, ameneyo anali Mkwatibwi wa Amitundu.

179 Tsopano kuti tiwerenge zina zonse tisanatseke. Apa pali nkhani yomvetsa chisoni kwambiri yomwe inu munayamba mwaiwonapo kumapeto kwa nthawi, pamene ife tikuthera tsopano, Mkwatibwi wa Amitundu wasankhidwa kale, watulutsidwa. Chinthucho chiri pafupi kumalizika. Tsopano mvetserani apa mu mutu wa 41. "Ndipo izo zinafika pochitika. . ." Izi ziri kumapeto kwa m'badwo wa Ayuda tsopano, ndiye ife tikutseka. "Kumapeto kwake, zaka ziwiri zathunthu, Farao. . ." Ayi, dikirani miniti, ine ndiri—ine ndatenga mutu wolakwika apa, ine ndikutsimikiza ndithu. 45, ine ndimafuna kutero, mmalo mwa 41.

> *Pamenepo Yosefe sanakhoze kudziletsa yekha pamaso pa onsewo amene anaimirira pafupi ndi iye; ndipo iye analira,* ndipo anapangitsa *munthu aliyense kuti apite* kutali *ndi* iye. *Ndipo panalibe munthu anaima ndi iye, pamene Yosefe anali kuzidziwitsa* yekha *kwa abale ake,* iwo amene anamukana iye.

180 Tsopano, mphindi yokha ife tisanachoke. Yosefe, zitatha zaka zonse izi, anali ali kumusi uko, uko kunayambika njala mdziko lakwawo, Mulungu akusuntha. Yosefe wamng'ono wosauka anadzakhala munthu wa dzanja lamanja. Ndipo apa, abale ake amene anamgulitsa iye, ine anali atawona masomphenya a iwo akubwera, akuweramira pamaso pake, ndipo iwo anamutcha iye wolota maloto ndi mpenyi wa masomphenya, ndipo anayesetsa kuti amuphe iye. Basi monga iwo. . .

181 Yesu ananeneratu kwa Ayuda amenewo, za chimene iwo anali ndi chimene iwo anachita, ndi chimene chikanati chidzakhale. Za Mbuye wa nyumbayo, anatumiza Mwana Wake Yemwe, ndi antchito Ake, ndi momwe iwo anawaphera Iwo, ndi chirichonse monga choncho. Koma kodi Ameneyo, Mbuye wa zokolola, akanadzachita chiyani pamene Iye adzabwera ndi kudzawapeza antchito oyipa amenewo? Tsopano, mphindi yokha.

182 Apa pali Yosefe, choyimira changwiro, atayima pamenepo monga Ayuda akubwerera mmasiku otsiriza, pa mapeto, akubwera kudutsa mu Zakachikwi, pamene Ayuda ati adzapulumutsidwe kachiwiri.

183 Ndipo iwo anayang'ana. Ndipo Yosefe, inu mukudziwa momwe iye anatumizidwira kumusi kumeneko, momwe a. . . Israeli anatumiza ana ake. Iwo ali ndi chimanga pang'ono; iwo anali akufa ndi njala, ndipo Yosefe anali atatanthauzira loto la mfumu, ndi momwe iye anali atasungira chimanga, malo okhawo mdziko amene anali ndi chakudya.

184 Ungwiro wa mpingo lero, malo okhawo Chakudya chauzimu chikuperekedwa, ndi mu Ufumu wa Yesu Khristu. Inu mukhoza kupita kukatenga zikhulupiriro zina zakale za mpingo ndi

kubwereza tizikhulupiriro tingapo ta atumwi, ndi chirichonse chimene inu mukufuna kutero, koma, m'bale, Mzimu ukugona mu Mpingo wobadwa-kachiwiri wa Mulungu wamoyo, ndi kokhako kumene kuli Chakudya. Ndipo Ayuda amenewo adzazindikira zimenezo limodzi la masiku awa, ndipo iwo akubwera.

185 Tsopano inu mukuzindikira, ndiye pamene iye anabwera, iye anati iye anamuwona Benjamini wamng'ono. Ndipo momwe, inu mukudziwa, momwe iye anachitira kumeneko, ndi kumvetsa. Momwe kuti abambo ake, amayi ake anabala mwana uyu, ndiyeno anali atafa, Benjamini wamng'ono, ndipo iye anamuwona m'bale wake. Ndipo iwo sankadziwa yemwe iye anali, ndipo iwo ankaganiza kuti iye anali kalonga wamkulu, ndipo iwo ankachita mantha. Ndipo kenako pamene iye anatumizanso, ndipo iye anati, "Ndinu ndani?"

186 Ndipo iwo anati, "Ndife ana a munthu mmodzi, amene ali Yakobo, amene ali wokalamba; inu mukudziwa, Israeli, ndipo yemwe anali wodalitsidwa wa Ambuye, ndi zina zotero." Ndiyeno iye anamva kuti abambo ake okondedwa achikulire anali akadali moyo. Mvetserani chimene iye ananena apa. Ndipo iye anadzizindikiritsa yekha kwa iwo pamene iye anatseka zitseko. Mtima wake, tayang'anani pa chikondi cha Mulungu pamenepo, chikuyitanabe. Ndipo apo Ayuda amenewo atayima pamenepo, anyamata osauka, iwo akufa ndi njala.

187 Bambo awo anali ndi njala, anati, "Pitani kumusi ndipo mukatenge chimanga chochulukirapo pang'ono, kapena tifa ndi njala."

188 Ndipo iye anamusunga Benjamini kumusi kumeneko ngati chizindikiro. Ndipo inu mukudziwa momwe izo zinachitikira, momwe iye anaima pamaso pake. Ndiyeno iye anayang'ana ndipo iye anamuwona Benjamini, iye sanathe kudziletsa kenanso. Iye anamupanga munthu aliyense amuchokere iye, achokepo. Ndipo Yosefe wosauka anaima pamenepo, ndipo iye anati, "Ine ndine Yosefe, m'bale wanu."

189 Ndipo abale ake anali atangomuuza kumene iye, anati, "Ife tiri naye m'bale mmodzi amene kulibe, amene anaphedwa ndi zirombo," ndipo iye anali akuyankhula kumene ndi m'bale wake. Ameneyo anali m'bale wake, Yosefe, yemwe anali atayima pamenepo.

190 Ndipo iye—anawapangitsa iwo onse amuchokere, kenako anadziulula yekha, iye anati, "Ine ndine Yosefe, m'bale wako." Ndipo iwo anachita mantha, mbadwayo. Iwo anachita mantha. Iye anati, "Musachite mantha ayi." Ndipo iye anayamba kukuwa mokweza kwambiri mpaka ngakhale mnyumba yachifumu ya Farao iwo anamumva iye akukuwa, anamva kukuwa kwake ndi kulira. Iye anathamangira pamenepo ndipo anaponyera manja ake mozungulira Benjamini wamng'ono,

ndipo anamukumbatira iye ndi kumupsyopsyona iye, ndipo anagwera pa khosi lake ndi kuyamba kulira, anati, "Iwe ukutanthauza kunena kuti abambo anga osauka akadali moyo ku Kanani?" Ndikumverera kotani kumeneko! Bwanji, chikondi cha Mulungu chimene chakhetsedwera kunja! "Bambo anga akadali ndi moyo ndipo ine ndikuwapatsa iwo chimanga china." Anati, "Oh!" Ndipo iye anafuula mokweza mawu ake.

191 Ine ndikudabwa chomwe icho chiti chidzakhale, tsiku limene Ambuye wathu Yesu adzatulukira kumeneko kudutsa mchizimezime chakummawa, akubwerera ku dziko lapansi kachiwiri. Aleluya!

192 Pamenepo iye anafuula ndi kulira, kalonga wamkulu uja atayima pamenepo, ndipo mbadwazo. Anati, iye anati, "Musadzikwiyire nokha." Anati, "Mulungu ananditumа ine." Mwaona Mzimu Woyera, momwe Chikondi Chaumulungu chiti chidzachitire? Anati, "Mulungu ananditumiza ine kuno. Musadzikwiyire nokha." Anati, "Mulungu ananditumiza ine kuno kuti ndidzasunge moyo kwa nthawi izi."

193 Ndipo kodi Mulungu anamutumizira chiyani Iye kuno, koma kuti adzasunge Moyo? Kodi Mzimu Woyera ndi wa chiyani kuno usikuuno, koma kuti udzasunge Moyo? Iye anakanidwa ndi Ayuda, ndipo anatumizidwa kuno kwa Amitundu, kuti akasunge Moyo. Kodi inu muli nawo Iwo usikuuno, mzanga?

194 Ndiye iye akuti, "Kodi bambo anga akadali ndi moyo?" Ndipo iye anatumiza kumeneko ndi ngolo ndi ng'ombe, ndi zina zotero.

195 Ndipo Israeli wosauka, wokalamba, wakhungu anatulukira, mneneri wokalamba akutulukira monga chomwecho, ndipo iye anamva kuti Yosefe anali moyo. Iye analira, ndipo iye anati, "Oh, Mulungu adalitsike! Ine ndidzamuwonanso mwana wanga, ndikumugwira iye."

196 Pamene iye anamubweretsa iye kumeneko, iye anakomana naye iye. Wakhungu wake wakale. . .zala zofooka zikutulukira monga choncho, ndipo anagwira nkhope ya Yosefe, ndipo iwo anagwada pa chinachake pamenepo, ndipo anayamba kulira ndi kukuwa. Atate ndi mwana, akukumbatirana wina ndi mzake. Oh, mai!

197 Pamene ine ndiganiza za wolowerera, usikuuno, amene ali kutali ndi Mulungu, kunja uko mu tchimo, m'bale, kumadyera mu khola la nkhumba, akuthamangathamanga kuzungulira dziko! Bwanji, bwanji inu osatero, mu nthawi ya chitsitsimutso ichi, ngati inu munawononga moyo wanu mu zaka zimenezi, mu moyo wachiwawa, ndi chuma chanu, bwanji inu tsopano osatembenukira, mu mtima mwanu, kwa Atate? Ngati inu mwachita chimene chiri cholakwika, bwanji osakumana naye Iye usikuuno, pakati pa njira, ndi kuponyera manja anu momukumbatira Iye.

"Mukuti, inu mukutanthauza kundiuza ine, M'bale Branham, Mulungu akundikondabe ine?"

198 Iye akufunafuna inu usikuuno. Iye akukuyang'anirani inu. Mzimu Woyera uli pano kuti udzasunge Moyo, kuti ukusungeni inu, kuti ukupatseni inu mdalitso, kuti ukusankheni inu. Ndipo ngati inu munasankhidwa mwa Mulungu, inu mwabwera kuno usikuuno ndi cholinga china.

Inu mukuti, "M'bale Branham, Kodi ine ndinadziwerengera ndekha zimenezo?"

199 Chifukwa chiyani inu mwabwera ku tchalitchi usikuuno? Nchiyani chinakupangitsani inu kubwera? Inu mukuganiza kuti mdierekezi angakukokereni konse inu ku tchalitchi? Ayi, bwana. Mdierekezi angakuchotsereni inu kwa izo. Mulungu wakhala akuitana. Ndi Atate akukuitanani inu usikuuno. Tsopano, inu muli nawo malo mwa Mulungu, ndipo Mulungu wayitana ndipo wayitana ndipo wayitana. Ngati inu simukulandira malo amenewo. . . Alipo malo ambiri owerengedwera kuno kwa aliyense, ndipo Mulungu anakonzeratu mmbuyo kutali uko kuti malo awa ayenera kukhalapo. Tsopano, ngati inu mutalephere kutenga malo amenewo, winawake adzawatenga iwo mmalo mwanu. Kotero, tsopano, ngati inu simunatenge malo anu usikuuno, Mulungu atapereka usikuuno kuti inu mutenge malo anu.

200 Mawa usiku tidzapita . . . Iwo anakhala ku Igupto kumeneko kwa zaka. Ndipo tsopano mawa usiku, ife tidzawatulutsa iwo pansi pa mwanawankhosa wansembe, ndi kuwabweretsa iwo kudzafika mpaka ku Yordano, ndiyeno nkudzawawolotsa iwo mtsinje, kudzalowa mu dziko lina la mchipululu.

201 Ambuye adalitse mmodzi aliyense wa inu. Izi zakhala zovuta usikuuno, izo zatenga nthawi yayitali. Izo zakhala zikupala ndi kukoka, pafupifupi ora ndi theka pano, kapena kupitirira, ndi—ndi kumadutsa mu Malemba, mwaukali ndi zimenezo. Koma, m'bale, mlongo, kodi inu mungazindikire usikuuno kuti ndi kusankha mwa Mulungu? Ndi angati amakhulupirira mu "kusankhidwa mwa Mulungu"? Ndi angati akukhulupirira kuti Mulungu amakusankha iwe ndipo amakuitana iwe, Iye ndi Mmodzi Yemwe amachita zimenezo? Tsopano ndinu okondwa? Kodi inu mukukhulupirira?

202 Kodi inu mukukhulupirira usikuuno kuti inu mukhoza kuima tsopano, mawa, ndi kunena kuti, "Satana, iwe wandikankha ine mozungulira, ndipo iwe wachita *ichi* ndi kuchita *icho*. Ndipo mu mtima mwanga, nthawi zonse, mwakhala muli Chinachake chikugunda, chikundiuza ine, kwa Mulungu. Tsopano ine ndikuzindikira chomwe kuyitana kwanga kuli. Ine sindidzakhutitsidwa nkomwe kunja uko. Ine sindingakhoze kukhutitsidwa kunja uko, chifukwa Mulungu wandiyitana ine. Kotero ine ndikukonzekera tsopano kutaya

zinthu izi kumbali, ndi kubwera kwa Atate anga Akumwamba. Ine ndidzakhala ndi Iye"?

203 Ndi angati muno akanafuna kunena kuti, "M'bale Bill, kuyambira usiku uno mpakana, Ine ndikudzilonjeza ndekha kwa Mulungu, kuti ine ndidzamutumikira Iye. Ine ndikudziwa ife tiri kumapeto kwa msewu, ndipo ine ndikudziwa kuti ife tiribe nthawi yochuluka kwambiri imene yatsalira. Koma mwa chisomo cha Mulungu, usikuuno, ine ndikutanthauza kuti ndipange kusesa moyera, ndipo ndimutumikira Mulungu"? Kodi inu mungakweze dzanja lanu? Mulungu adalitse mtima wanu. Chabwino.

204 Ndi angati omwe mukumverera kuti munganene kuti, "M'bale Bill, ine ndiribe izo mmalingaliro anga ndendende basi. Koma kodi inu mungandipempherere ine, kuti Mulungu akakhale nane kumeneko pa tsiku limenelo, kuti Mulungu andipatse ine kuitana kumodzi kwinanso mu mtima mwanga? Ndipo ine ndibwera ngati Iye atangondiyitana ine kamodzinso, ine ndibwera"? Kodi inu mungakweze dzanja lanu? Kodi inu mukukhudzidwa kwambiri ndi izi usikuuno? Mulungu akudalitseni inu, dona. Mulungu akudalitseni inu, dona. Winawake tsopano anene...? Kwe-...Mulungu akudalitseni inu, dona. Mulungu akudalitseni inu, bwana. Mulungu akudalitseni inu. Ndipo Mulungu akudalitseni inu, dona wamng'ono.

205 Winawakenso akuti, "M'bale Branham, ine sindiri chimene ine ndiyenera kukhala usikuuno. Ine ndikudziwa ine sindiri ayi. Ine ndamukwiyitsa Ambuye wanga, koma Chinachake mu mtima mwanga chakhala chikundiuza ine kuti ine ndikuyenera kukhala Mkhristu. Ndipo ine ndikufuna kumutumikira Mulungu." Kodi munthu ameneyo ali pano usikuuno, ndipo sanapange kuyamba kumeneko? Tsopano, ine ndikufuna kuti inu mukhale owonamtima ndi ine pakali pano, potseka, amene mukudziwa izi. Kuti, Chinachake m'moyo mwanu chakuuzani inu kuti muyenera kutumikira Mulungu, inu mwamverera monga chomwecho kwa nthawi yaitali. Inu simunapangebe kuyambako panobe, koma Chinachake chakuuzani inu zimenezo.

206 Ine, ine sindine mmodzi wa anthu amene ndingathamangire kumbuyo uko ndi kudzakukokerani inu kuno. Ayi, ayi. Ngati Mzimu Woyera, kupyolera mu kulalikira kwa Mawu, suchita zimenezo, sizindichitira ine ubwino uliwonse. Mwaona, ndiko kulondola, inu muyenera kupanga kusankha kwanu.

207 Koma kodi inu mudzakhala woona mtima mokwanira ndi ine, ndikuti, "M'bale Bill, pakhala pali Chinachake mwa ine kwa zaka, kapena nthawi, kapena chirichonse chimene chiri, chimene chandiyitana ine, chimene chandiuza ine, zinkawoneka ngati ine ndiyenera kutembenukira kwa Mulungu, ndipo ine sindinachite

izo panobe. Inu mundipempherere ine, M'bale Bill, kuti—kuti ine ndikhale mwamuna kapena mkazi wokwanira kuchita izo?" Kodi inu mungakweze dzanja lanu? Paliponse mchipindachi tsopano, amene mukumverera kuti—kuti Mulungu. Mulungu akudalitseni inu.

208 Winawakenso akuti, "Chinachake chayitana pa mtima panga ndipo ine sindinayambe ndapangapo kudzipereka kwanga panobe." Ingokwezani dzanja lanu, ndikuti, "Ine, ndine ameneyo. Ine sindinakhalebe Mkhristu, koma ine—ine—ine ndikufuna kutero. Ine ndikufuna kutero, ndipo ine ndikufuna kuti inu mupemphere kuti—kuti Mulungu asadzandikane ine mpaka nditapanga chigamulo changa." Kodi inu muchita zimenezo? Kwezani dzanja lanu. Mulungu akudalitseni inu, bwana, izo nzabwino mwamphamvu. Basi winawake kwezani dzanja lanu, ndikuti, "Ine—ine ndikufuna kuti inu mupemphere, M'bale Bill, kuti ine—ine sindidzamukana Mulungu." Mulungu akudalitseni inu, bwana. Kuti, izo nzabwino. Tsopano winawakenso. Kodi alipo winawakenso muno. Tsopano, mukhale owona mtima.

209 Tsopano taonani, bwanji ngati dokotala atabwera kunyumba kwanu kusanache, iye nkudzatenga kugunda kwa mtima kwanu, nkubwerera mmbuyo, nkudzati, "Ayi, iye sadzatuluka mwa izo, iye watheka"? Oh, momwe inu mukanafunira kuti mukweze dzanja limenelo mmwamba!

210 Izo zikhoza kutanthauza chinachake, mukanati, "Mundipempherere ine, m'bale." Ine sindikudziwa yemwe inu muli, pokhapokha ngati inu mutandididziwitsa ine. Mpingo sukudziwa yemwe inu muli. Koma ngati inu mutakweza mmwamba dzanja lanu, Mulungu azizindikira zimenezo. Izi sizingakupulumutseni inu, ayi, koma izo zidzakupatsani inu kuchuluka kwa kuyamba. Izo zidzakupatsani inu kuyamba kochuluka chomwecho. Ndiye mwinamwake chitsitsimutso chisanathe, inu mupereka mtima wanu kwa Khristu.

211 Tsopano, izi zakhala zovuta usikuuno. Ife tiyesetsa kupita pansi mochuluka mu zolimba, mpaka kudzalowa mu Mawu pachiyambi, ine ndikutanthauza, pamene ife tikupitirira.

212 Kodi alipo mmodzi winanso? Pakhala pali faivi atakweza manja awo. Winawakenso? Kodi ine ndingangokhala ndi sikisi kapena seveni okha? Tsopano, ine ndikufuna inu mukhale owonamtima. Mulungu akudalitseni inu, dona wamng'ono. Tsopano, ine ndikudziwa kuti aliponso munthu winanso mkati muno yemwe akuyenera kukweza dzanja lake mmwamba. Tsopano, ingokwezani dzanja lanu mmwamba, ndikuti, "M'bale Bill, mundipempherere ine." Ine—ine sindibwerera kumene inu muli, ine ndikupemphererani inu pomwe pano. Ndiyeno mungonena kuti, "Ndikumbukireni ine tsopano, kuti ine sindine Mkhristu, koma ine ndakhala ndikumverera kuti ine ndiyenera

kukhala. Ndipo tsopano ine ndikudziwa ine sindine Mkhristu." Kodi alipo wina tsopano, ikani dzanja lanu mmwamba. Eya, ndikukonzekera kuti nditseke. Pitani ku limba, Teddy, ngati inu mungatero.

213 Winawake akuti ndiye, "M'bale Bill, ndikumbukireni ine, kuti moyo wanga uyandikire pafupi ndi Mulungu. Ine— ine sindikufuna kukhala, kukhala moyo watheka uwu ndi chikhalidwe chofunda ichi. Ine ndikufuna kutero, kwenikweni, mtima wanga ukuyaka moto. Mundipempherere ine." Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu, inu, inu. Izo ndi zabwino. Ndi zabwino. Mulungu akudalitseni inu. Ine ndikuwona manja anu akukwera mmwamba.

214 Taonani, ngati Mulungu amamva pemphero langa kuti amatsegule maso a akhungu, kutsegula makutu a ogontha, kuwapanga iwo amene ali olumala (congressmen, mafumu, amphamvu, mafumu, olumala) basi kungowawongola! Yang'anani kuzungulira dziko lapansi, mamillioni, mamillioni! Ine ndingakonde kunena ichi, ndi moona kuchokera mu mtima mwanga, pafupifupi anthu mamillioni teni amene ine ndikuwadziwa anamva Uthenga, anthu mamillioni teni a mafuko onse. Ine ndayankhulapo pamaso pa mafuko teni ndi fifitini nthawi imodzi, kuchita kudutsa otanthauzira teni kapena fifitini iwe usanafike poti unene mawu ena, basi monga chomwecho kudutsa mwa otanthauzira. Ndipo kuwona ochuluka ngati handiredi sauzande, kapena, ndi kuwona ngati sarte sauzande pa nthawi imodzi akubwera kwa Khristu, sarte sauzande otembenuka nthawi imodzi. Durban, South. . .

215 Ndipo ine ndikupita ku msonkhano tsopano kumene anthu sarte sauzande adzakakhalako. Ndipo ine ndikunena izi kuchokera mu mtima mwanga. Kodi inu munayamba mwandimvapo ine ndikuneneratu chirichonse mu Dzina la Ambuye koma chimene chinali ndendende basi mwanjira imeneyo? Funsani kulikonse komwe inu mungafune, kulikonse padziko lapansi. Ndipo muyang'ane pa mahandiredi ndi mahandiredi a zinthu zomwe Iye ananena. Ndithudi, ine ndikudziwa zomwe ine ndikuzikamba. Osati kwa ine ndekha; Khristu mkati *muno*.

216 Ndipo ine ndikukuuzani inu Choonadi, abwenzi, ngati mutafe popanda kubadwanso mwatsopano, inu mwataika. Yesu anati, "Kupatula ngati munthu atabadwa mwa madzi ndi Mzimu, iye sadzalowa konse mwanjira iliyonse mu Ufumu." Ziribe kanthu momwe iwe uliri wabwino, ndi zochuluka chotani zomwe inu mwalipira, ndi mpingo wanji umene inu mulimo, chomwe ubale wanu unali, chimene chikhalidwe chanu chinali, chimene amayi anu kapena abambo anu anali, chimene abusa anu anali. "Pokhapokha munthu atabadwa mwatsopano, iye sadzawuwona konse Ufumu wa Mulungu."

217 Ife tinatenga chimanga chimenecho tsiku lina, inu munachiwona icho kuchokera kuno ku ulimi. Chimodzi cha icho chinali njere yangwiro ya chimanga, kuchuluka kulikonse kwa kashiamu, chirichonse chinali mu njere *iyi* chinali mu njere *iyi*. China chimakulira mmunda ndipo china sichinali, chokwanira mdzanja pa chirichonse. Iwo anachikwirira icho. Panalibe chimodzi chomwe chinapangidwa ndi chosakaniza chirichonse chomwe chinali mwa chinacho, chinapangidwa, chowumbidwa mofanana, ndi chirichonse. Palibe chimodzi cha *icho* chimene chinamera. Koma chimodzi chirichonse cha *ichi* chinamera. Chifukwa chiyani? Icho chinali ndi nyongolosi ya moyo mwa icho.

218 Pali amuna ndi akazi pano usikuuno tsopano, ndi padziko lonse, amene akumapita ku matchalitchi awo, ndi a mpingo, akudzinenera kuti ndi Akhristu, ndipo alibe nyongolosi ya Moyo mwa iwo. Iwo sangakhoze kubwera. Palibe njira yoti iwo angadzuke. Usati unyengedwe, mzanga, dziyese wekha. Izo ziri ndi inu. Izo ziri mwa inu. Ndi chisankho chanu. Ambuye akudalitseni inu pamene ife tikuweramitsa mitu yathu.

219 Atate, ntchito iyi usikuuno, ine—ine ndinayenera kunena zinthu zovuta, zinthu zowawa, zodula molimba, koma Inu munati Uthenga ndi wakuthwa kuposa lupanga lakuthwa konsekonse, kupyoza ngakhale m'mafupa a m'mafupa, ndi Wozindikira zolingirira za mumtima. Mulungu, aletse kuti ife tikhale ndi chirichonse chochepera kuposa Icho. Tsopano, ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha "kusankhidwa," ife tikukuthokozani Inu kuti Inu mwatiyitana ife. Ndipo tsopano, mmitima yathu, Mzimu Woyera watisunga ife zaka zonsezi. Momwe ife tikukuthokozerani Inu! Chisomo chodabwitsa, kuganiza kuti ife tinatuluka mngalande za tchimo, mmbuyo momwe mmasiku, ndi momwe kuti Inu mwakhalira wabwino kwa ife.

220 Ndipo Inu mukuwakonda amuna ndi akazi awa omwe ali pano mdzikoli tsopano, podziwa kuti kwatsala pang'ono kutembenuka kwa dzuwa ndipo nthawi idzakhala itatha nthawi imeneyo. Limodzi la masiku awa nthawi idzakhala itatha kwambiri. Iwo adzadulidwa, ndipo mwaliwiro chomwecho, popanda chithandizo, popanda chifundo, ndipo Inu munanena kuti Inu mudzangoseka mu masautso a iwo.

221 Kuganiza za dziko lino, limodzi la masiku awa mphepo zowomba zidzawomba kudutsa dziko lakale lino, pamene ilo lidzaphulitsidwe ndi bomba la atomiki, liri kutaliko mu mlengalenga mwa dzuwa, ndipo mphepo zowomba zikuwomba modutsa, zaka faivi handiredi kuchokera usikuuno. Ndipo padzakhala miyala ya pamanda itabisidwa mu mchenga umenewo, ndi mwinamwake maina athu pa iyo, itagona kutsidyako mu kamvuluvulu ndi mkokomo, ndi mphepo,

kutentha kophulika kochokera ku dzuwa. Koma kodi moyo wathu wosauka udzakhala uli kuti?

222 Mulungu, mulole uwu ukhoze kukhala usiku umene kopita Kwamuyaya kwina kwagamulidwa. Perekani, Ambuye, kuti wochimwa aliyense muno, amuna amenewo ndi akazi, ndi akazi aang'ono ndi ena otero, amene anakweza manja awo ndipo anati iwo anali ochimwa ndipo amafuna kuti akumbukiridwe mu pemphero, O Mulungu, mulole Mzimu Woyera upereke izo pakali pano. Ndipo mulole iwo amulandire Yesu Khristu ngati Mpulumutsi wawo, akhale odzazidwa ndi Mzimu Woyera.

223 Perekani, Ambuye, kuti obwerera mmbuyo awa, ndi awa omwe ali ozizira ndipo achoka kwa Inu, mulole iwo abwere akuthamanga usikuuno monga gulu la ana omwe akufa ndi njala, akuthamangira ku Gome la Mulungu, akuti, "Ine ndikufuna kudyetsedwa." Ndipo Inu mutakachita zimenezo, Ambuye.

224 Ndipo zikomo Inu chifukwa cha oyera okondedwa awa a Mulungu amene akweza manja awo mmwamba, ndipo kupyolera mmisozi ndi pemphero, ndipo akupitirira, iwo akhala okhulupirika mpaka ora lino.

225 Mudalitse mawu awa usikuuno, Ambuye, ngakhale iwo athamanga kuchokera ku mbali imodzi ya Baibulo nkupita kwa inayo, ndi zonse zolakwitsa, ndipo mwinamwake Inu mukhoza kuzikonza izo mmalingaliro awo, Ambuye. Izo zakhala zatsopano kwa ine, nthawi yoyamba kwa zaka seveni, Ambuye, kuti ndidzayesere izi. Ndipo ine ndikupemphera tsopano kuti mawa usiku Inu mutibweze ife tonse, ndi zochulukirapo, ndipo mulole Mzimu Woyera ukhale pano. Ndipo ambiri a awa pano usikuuno akapanga chigamulo ndi kupulumutsidwa, adzabwerera mawa usiku, akusangalala ndi okondwa, (perekani izi, Ambuye) kugwera pa khosi la Atate, monga Yosefe anachitira, Ambuye, kuwapysopysona Atate, oh, ndi kunena kuti, "Zikomo Inu, Ambuye, chifukwa chondipulumutsa ine." Perekani izi, Ambuye. Mulole chinachake chichitike tsopano. Ife tikupempherera dalitso ili, kuti inu mutibalalitse ife ku msonkhano uno, koma osati nkomwe kuchokera Kwanu—kuchokera Pamaso Panu, ndipo mulole ife tibwerere, okondwa, osangalala, mawa usiku, tikubweretsa mitolo yofunika. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Khristu. Ameni.

226 Mzanga wa Chikhristu, ine ndikupepesa kuti ine ndakusungani nthawi yonseyi. Ndine wopepesa kwambiri. Mawa usiku ine ndikukonzekera kudzatuluka pa naini koloko, ngati nkotheka. Ine ndimayenera kuyankhula mwaukali pang'ono. Ine sindikanatha kuzithandizira izo. Inu mumandikonda ine, mulimonse, sichoncho inu? Ine ndikutero, Ine ndimakukondani inu. Ndipo ndi za ubwino wanu wokha.

Tsopano kodi ife tingayime. Chabwino, *Tenga Dzina La Yesu Nawe,* poyambira.

Tenga Dzina la Yesu nawe,
Mwana wachisoni ndi watsoka;
Lidzakupatsa chisangalalo ndi chitonthozo . . .

227 Tsopano, ine ndikufuna kuti inu mudzakhale pa telefoni mawa. Mukampeze munthu wina wochimwa, mudzambweretse iye. Mudzabwererenso. Mukawauze azibusa. Bwerani tsopano, tiyeni tigwirizane limodzi ndi kudzakhala ndi chitsitsimutso chachikale. Ife tidzawongoledwa mu usiku umodzi kapena uwiri, tsopano, kotero ife tipitirira ndi kukhala ndi nthawi yabwino. Gwiranani chanza wina ndi mzake tsopano.

. . . Kumwamba;
Dzina lofunika, O ndi lokoma bwanji!
Chiyembekezo cha padziko lapansi ndi chimwemwe cha Kumwamba.

228 Tsopano mulole chisomo cha Mulungu, ndi chiyanjano cha Mzimu Woyera, chikhale ndi kukhala ndi inu, kuyambira tsopano mpaka ife tidzakomanenso, mu Dzina la Yesu. Ameni.

229 Mulungu akudalitseni inu tsopano. Inu mwabalalitsidwa, mu chikondi ndi mdalitso wa Mulungu. Tsopano, inu nonse mamembala a kachisiyu, gwiranani chanza ndi anthu awa pano. Muwonetsetse kuti aliyense wa inu agwirane chanza, ndi kuwalandiranso iwo. Mulole Mzimu Woyera uchite chimodzimodzi. Tsopano ingokonzani izo, muyiwale kutsemphana kwanu konse, ndi kuzikonza izo. Chabwino.

Pa Dzina la Yesu kugwada,
Kudzigwetsa . . .

53-0325 Israeli Ndi Mpingo #1
Branham Tabernacle
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org